Baptist Publishing House
OF THE BAPTIST MISSION OF ZAMBIA
P.O.BOX 1095 LUSAKA

# Kukula monga Akristu

verna savage

ZOWERENGA ZA M'CIPANGANO ZA TSIKU NDI TSIKU:

Mwezi Wacitatu:

1. Macitidwe 1:8
2. Aroma 10:9-13
3. Mateyu 25:1-13
4. Mateyu 12:30
5. Yohane 1:12
6. Mateyu 10:32
7. Luka 12:8
8. Tito 3:5
9. Miyambo 28:13
10. Aefeso 2:8-9
11. Tito 3:5
12. 1 Timoteo 1:9
13. Ahebri 7:18-19
14. Akolose 1:14
15. Agalatiya 6:7-8
16. Yohane 10:9
17. Yohane 16:6
18. Macitidwe 4:11-12
19. Tito 1:16
20. 1 Timoteo 2:5
21. 1 Yohane 2:1
22. Yohane 20:31
23. 1 Akorinto 8:5-6
24. Miyambo 11:30
25. 1 Timoteo 1:15
26. Mateyu 11:28-39
27. Aroma 14:12
28. 1 Yohane 2:17
29. Danieli 12:3
30. 2 Timoteo 3:16
31. Yohane 20:31



# Kukula monga Akristu

verna savage

ZOWERENGA ZA M'CIPANGANO ZA TSIKU NDI TSIKU

Mwezi Waciwiri:

1. Mateyu 18:19
2. Yohane 3:34
3. Macitidwe 4:12
4. Aroma 12:1-2
5. Agalatiya 5:13
6. 2 Timoteo 1:7-8
7. Masalmo 19:14
8. Mlaliki 11:6
9. 2 Timoteo 4:2
10. Yohane 3:3
11. Miyambo 24:10-12
12. Aroma 3:23
13. Agalatiya 5:20-21
14. Yakobo 4:17
15. 1 Yohane 16:8
17. Aroma 10:13
18. 1 Yohane 1:8
19. Yesaya 64:6
20. Yohane 3:36
21. Yohane 3:18
22. Aroma 6:23
23. Marko 10:17-31
24. 1 Yohane 1:9
25. Yohane 9:41
26. 1 Akorinto 6:20
27. 2 Akorinto 5:20
28. Macitidwe 4:12
29. Luka 13:3
30. Masalmo 51:17
31. Yesaya 53:6

ZOWERENGA ZA M'CIPANGANO ZA TSIKU NDI TSIKU.

Mwezi Woyamba:

1. 2 Akorinto 5:14-17
2. Mateyu 4:19
3. Ezekieli 3:18
4. Luka 19:10
5. Mateyu 28:20
6. Marko 8:34
7. Yohane 15:5
8. 1 Yohane 1:9
9. Aroma 12:1-2
10. Yohane 3:11
11. Yohane 3:3,6-8
12. Aroma 10:9-10
13. Yohane 1:12
14. 1 Yohane 3:14
15. Aroma 8:14-16
16. Macitidwe 22:14-15
17. Macitidwe 4:13
18. Aroma 1:16
19. 1 Yohane 5:14-15
20. Yesaya 55:11
21. 1 Akorinto 13:4-8,13
22. Macitidwe 5:32
23. 1 Petro 1:23
24. Yesaya 55:10
25. Luka 4:4
26. 1 Petro 2:2
27. Masalmo 119:11
28. 2 Akorinto 4:3-4
29. Ahebri 4:12
30. Masalmo 119:105
31. Luka 18:1



ZA M'KATIMU


MAU OYAMBA — TSAMBA

PHUNZIRO

1 MAZIKO A KUKULA MWA CIKRISTU........ 2

2 KUPITIRIZA KWATHU KWA KUMVERA KRISTU........ 7

3 AKRISTU AMAKULA KUPYOLERA M'ZOBVUTA........ 12

4 AKRISTU AMAKULA KUPYOLERA MUKUPHUNZIRA........ 17

5 AKRISTU AMAKULA KUPYOLERA MU CIYANJANO........ 23

6 AKRISTU AMAKULA KUPYOLERA MU KULAMBIRA........ 29

7 KUKULA MWA CIKRISTU KUPYOLERA MU KUTUMIKIRA........ 34

8 CIKHALIDWE CATHU CA UCIMO..... 40

9 KUKULA M'CIKHULUPIRIRO........ 47

10 KUKULA M'KUDZILANGA WEKHA .... 52

11 KUKULA M'CIDZIWITSO NDI CIPIRIRO........ 59

12 KUKULA M'CIKONDI CA KRISTU.... 64

Mulungu atilamulira kuti tidzikondana wina ndi mnzace. Iye sananene kuti, "Mudzikondana ndi ao amene ali a pfuko limodzimodzi lanu ndi khungu limodzimodzi monda inu muliri." Dadanena kuti, "Mudzikonda ophunzira okha, acuma okha, ndi amene ali pamwamba." Iye anati, "Mukondane wina ndi mnzace," monga ndakonda inu." Tidzikonda anthu onse, anthu amitundu yonse, mapfuko onse - ali yense. Pamene Akristu onse mu dziko lapansi, osanena mtundu kepana khungu la matupi ao, angagwade pa guwa limodzimodzi ndi kulambira Mbuye wao pamodzi dziko lathuno lidzakopedwa kudza kwa ambiri mu dziko lathu lero ndi cifukwa cakusowa cikhulupiriro mwa anthu amitundu ina.

MTSOGOLERI:

Kodi muli olola kukonda mzimai mnzanu monga Kristu akukondani inu? Kodi muli olola kuonetsa cikondi ca Kristu m'moyo wanu kotero kuti ena aone Kristu mwa inu? Tiyeni wina ali yense wa ife awerame mutu kwa mphindi zowerengeka kupemphera pemphero la kacetecete kupempha Mulungu kuti atithandize kuti ticite cifuniro cace tsiku liri lonse la moyo wathu.

Kodi Kristu adapanga kusintha kotereku m'moyo mwanu?

Anthu amu Africa amakhala ndi mantha a zinthu zambiri. Mantha akuopa mizimu yoipa, mantha a ambala ndi olanda, mantha amene angawaopse ndi kuopsa miyoyo yao, mantha akuti sanatha kupeza malo m'skulu mantha kuti sanapeza nchito, mantha a matenda, mantha a imfa. Mantha ena ambiri oterewa tidawacitapo enafe. Pena a alipo ena a ife omwe ali kuopa ciweruzo comwe cizadza akafa. Koma Mkristu yemwe ali ndi cikhulupiriro colimba mwa Mulungu amene amatikonda alibe cifukwa cakucitira mantha. Mulungu wathu ndiye cikondi ndipo komwe kuli cikondi cangwiro sikungakhale mantha enieni.

GAWO LACINAI:
Kukula M'cikondi Ca Cikristu.

Cifukwa ca cikondi ca Mulungu kwa ife tidayenera kukula m'cikondi ca Cikristu.

Yohane ananena kuti ngati tikonda abale athu tabadwa a Mulungu. Cikondi ca wina ndi mnzace ndi cizindikiro ndi cionetse ca kubadwa kwathu ndi cidziwitso ca Yesu Kristu.

Pafunsidwa mafunso ambirimbiri za wotembenuka asanabatizidwe kuti aone ngati munthu wotembenukayu wapulumutsidwadi. Koma, kodi alipo wina yemwe anafunsidwa funso lotere, "Kodi ukonda mnzako?" Ili ndilo linali yeso la Yohane. Ngati munthu amapambana yeso limeneli anadziwadi kuti anasinthadi ndi kuti ali nao moyo wa tsopano mwa Yesu.



MAU OYAMBA

Kwa milungu khuni ndi iwiri iri nkudzayi tidzakhala tiri kuphunzira za Kukula monga Akrsitu. Maphunzirowa adzagawikana m'mbali zinai: (1) Kutanthauza kwa Kukula m"Cikristu, (2) Momwe Akristu Amakulira, (3) Zobvuta mu Kukula mwa Cikristu ndi (4) Mbali za Kukula mwa Cikristu. Maziko a Kukula kwa Cikristu ndi Yesu Kristu ndi kuyankha kwa munthu nthawi zonse kupyolera mu nchito ya Mzimu Woyera. Njira zina zomwe Akristu akulira ziri mu mabvuto, kuphunzira, ciyanjano, kupembedza ndi kutumikira. Maphunzirowa adzakhudzanso za momwe Akristu angakulire mu zobvuta za mkhalidwe wa anthu ndi munthu payekhapaykha. Mbali zina za kukula m'Cikristu zomwe tidzaphunzira zidzakhala za cikhulupiriro, kudzisungira wekha, cifatso ndi cikondi.

Lero lino mipingo yathu iri ndi mbali yofunika kwambiri kuti icite mu kukula kwa munthu. Tiri nazo nyumba zopemphereramo, Nyumba Yofalitsa ya A Baptist, Bibleway Correspondence, umboni wa pa wailesi ndi wailesi wa kaneka (Television), Sande Sukulu, nchito ya azimai, misonkhano ya kupembedza, ma kampeni a ulaliki zonsezi ziri za colinga cimodzi ndico: kukula kwa Mkristu aliyense payekha. Tipemphere kuti maphunziro amenewa adzakhale cotsogolera cacikuru mu kukula mwa Cikristu kwa munthu aliyense kupyolera mwa mphamvu ya Mzimu Woyera.

potumiza Mwana wace mmodzi yekha mu dziko lapansi. Ici ndico cinali cinthu coposa zonse comwe Mulungu akadacite, koma cidamtengera Mwana wace mmodzi yekha. Kupyolera mwa Yesu Kristu tikhoza kufika kwa Mulungu Atate.

Mu cikondi cimeneci, sikuti tingokonda Mulungu koma kuti anatikonda ife natitumizira Mwana wace kuti adzakhale ndipo la macimo athu, ndipo cifukwa ca cikondi cimeneci kwa ife anatipatsa njira yokhayo ya cipulumutso.

Cikondi cathu kwa Mulungu cimacitidwa ndi kupangidwa kukhala ca ngwiro pamene tiri kumacita cikondi cathu kwa wina ndi mnzace.

GAWO LACITATU:

Cikondi ca Mulungu Mwa Ife.
(1 Yohane 4:13-21).

Mulungu anatipatsa mzimu wacewace. Ao amene anaona momwe mzimuyu acitira akhoza kucitira umboni. Dziko pena silingamvetse, ndiponso zoonadi wocimwa sangathe kumuona Mulungu, koma ife Akristu timadziwa kuti Mulungu amakhaladi nafe.

Akristu ogwira nchito ndi odzipereka zisonyeza popanda kuaika kuti Mulungu anatumiza Mwana wace mu dziko lapansi. Iwo anakhala nao moyo wa tsopano mwa Yesu. Miyoyo yosinthika ndiyo zoonetsera cikhulupiriro ca Cikristu. Pali ponse pomwe pali gulu la Akristu pali ao amene myoyo yao inasinthika kwambiri cifukwa ca cikhulupiriro cao mwa Kristu kotero kuti anthu amanena kuti kusintha kotereku kungacitike ndi Kristu yekha.

cokoma. Mu Marko 3:17 tiwerenga pomwe Yesu anamucha Yohane mbale wanga, Yakobo, "Boanerges" comwe citanthauza "ana a bungu". Anali aukali (amtima wasontho) kotero kuti anafuna kuitana moto kuti utsike kucoka kumwamba kucoka mudzi wa mu Samariya womwe sunamulandire Yesu. Koma cikondi ca Yesu Kristu cidamusintha Yohane. Mu uthenga wonsewu Yohane alankhula za cikondi. Mbiri inena za mau otsiriza a Yohane. Pamene anali gone ali kufa, abwenzi ace anamufunsa ngati anali ndi mau amene anafuna kulankhula kwa iwo. Ndipo iye anati, "Ana ang'ono inu, kondanani wina ndi mnzace." Anawabwereza mau amenewa nthawi zambiri. Ndipo iwo anamufunsanso ngati zinali zokhazo anali nazo zakuti alankhule, ndipo iye anati, "Zakwana zomwezo, cifukwa ndi lamulo la Ambuye."

GAWO LACIWIRI:
Kondanani Wina Ndi Mnzace.
(1 Yohane 4:7-12).

Yohane atiuza kuti Akristu adzikondana wina ndi mnzace kotero kuti tikhale mmodzi mwa Kristu. Iye anena kuti tiri ana a Mulungu ndipo Mulungu ndiye cikondi; cotero, tiyenera kukondana wina ndi mnzace. Mulungu ndiye cikondi; ngati munthu wina ali ndi cikondi mu mtima mwace cicokera kwa Mulungu.

Yohane akuti munthu amene anena kuti konda Mulungu nadana naye mbale wace ali wabodza!

Ngati timdziwadi Mulungu tidziwano cikondi.

Mulungu ndiye cikondi ndipo anaonetsera cikondi cace kwa anthu. Anacita izi



PHUNZIRO 1

## MAZIKO A KUKULA MWA CIKRISTU

Nthawi yathu ndi Mulungu:

Nyimbo la Azimai ndi vesi:

Vesi loloweza: *"Pakuti palibe munthu akhoza kuiko ena, koma amene aikidwako, ndiwo Yesu Kristu."*
*1 Akorinto 3:11.*

Lemba lowerenga: 1 Akorinto 3:3-10.
2 Akorinto 5:14-17.

Pemphero:

MTSOGOLERI:

Nyumba ya Malamulo imene iri muno mu Lusaka ndi imodzi ya zinyumba zokongola kwambiri muno mu Zambia. Pamene muli kuyenda ndi galimoto kulowa mu Lusaka, makamaka pa nthawi ya usiku, ndico cinthu coyambirira comwe munaciona. Iri pamwamba pa kaphiri komwe kamaipangitsa kuti ikhale pamwamba pa zonse mu mzinda. Ma tani ambirimbiri a zitsulo ndi simenti zinankha m'maziko ace a cinyumba cimeneci. Omwe anaimanga anali akatswiri opambana okha amene anapezeka ndipo iwo anadziwa kufunika kwacekwa kuti amange maziko amphamvu ndi olimba.

Ngakhaletu amisiri omanga omwe sadziwa kanthu kwambiri amadziwa kuti maziko abwino ali ofunika kwambiri kuti amange nyumba ya bwino. (Werengani 1 Akorinto 3:16). Apa Paulo atiuza kuti Mkristu ali kacisi wa Mulungu ndikuti Mulungu amakhala mwa iye. Ndipo cotero maziko opambana kwambiri pa dziko lapansi ndiwo moyo wa

Cikristu. Kumbukiranitu kuti maziko akuru ali ofunika kwambiri ku nyumba ya ikuru. Nanga ndi maziko otani omwe moyo wa Cikristu wamangidwapo?

GAWO LOYAMBA:
Zizindikiro za Kupanda Kukula mwa Cikristu.
(1 Akorinto 3:1-4).

Pamene Paulo anali pa ulendo wa ciwiri anapita ku Korinto. Iye anagwira nchito mu mzinda wa ukuruwu kwa miezi khumi ndi isanu ndi itatu (18). Ndipo kupyolera mu nthawi imeneyi mpingo unakhazikitsidwa. Iwo unakhala mpingo waukuru kwambiri.

Zaka zitatu zapatsogolopo pamene Paulo anali ku Efeso iye anamva za mabvuto oposa omwe anali mu mpingo wa ku Korinto. Ndipo cotero iye analemba kalata kuwathandiza mabvuto awo. Mpingo unali wagawikana mbali zinai ndipo kusadzisunga (zigololo) zinalowa mu mpingomo. Ziwalo za mu mpingo zinali kumenyana zokha. Panali mabvuto a zamaukwati. Ndipo ena anali kumafunsa za utumwi wa Paulo yemwe kuti unali wotani. Iwo anali ndi mafunso a zobvala zoyenera pa nthawi ya kupembedza, za zinthu za mpatso za mzimu ndi kuukanso kwa okhulupirira.

Pamene Paulo anamva zonse zimenezi iye anawaca iwo kuti "ana amakanda mwa Kristu." Iwo sanakule monga Akristu. Iwo anali kumacita monga anthu wamba osati monga zilengedwe za mwa Kristu.

GAWO LACIWIRI:
Zida za Mulungu za Kukula mwa Cikristu.
(1 Akorinto 3:5-9).

Apa Paulo ali kulankhula za zincito zosiyana za atsogoleri mu nchito ya ufumu



PHUNZIRO 12

KUKULA MCIKONDI CA CIKRISTU

Nthawi yathu ndi Mulungu:

Nyimbo ya Azimai ndi vesi:

Vesi loloweza: *"Lamulo langa ndi ili, kuti mukondane wina ndi mnzace, monga nda, konda inu."*
*Yohane 15:12.*

Lemba lowerenga: 1 Yohane 4:7-21.

Pemphero:

MTSOGOLERI:

Kunali ao amene anali kuphunzitsa kuti Yesu anali munthu wina wamba. Pamene Yohane anamva ici analemba kalata yemwe anacedwa Yohane Woyamba. Yohane anaphunzitsa kuti Yesu Kristu anali Mulungu ndi munthu; ndi kuti Mulungu anali kuunika ndi moyo; ndikuti kuposa zonse - Mulungu ndiye Cikondi. Kristu anadza monga cionetsera ca cikondi cangwiroci. Iye anali Mwana wobadwa yekha wa Mulungu ndipo ifeyo ndife ana a Mulungu.

GAWO LOYAMBA:
Mtumi Wa Cikondani.

Yohane anali mmodzi wa ophunzira khumi ndi awiri a Yesu. Iye anali kukhala pafupi ndi Yesu ndipo anali kumacedwanso mmodzi wa atatu omwe anakhalitsa pambali pa Yesu.

Yohane anadziwika ndikuti "mtumwi waCikondano". Yohane analibe cibadidwe

Mkristu adzakhala nao mu mtima mwace mtendere womwe uposa cidziwitso conse. Kristu anadza pa dziko lapansi kuti adzetse mtendere ndi cidziwitso kwa anthu amitundu yonse.

Ife monga Akristu, tidzionetsera cikondi ndi mtendere wa Kristu m'mitima yathu.

MTSOGOLERI:

Tiyeni tipemphere kuti Mulungu atithandize kukhala opirira ndi a cidziwitso ku azimuna athu, ana athu, abwenzi athu ndi ao onse amene tikomana nao tsiku ndi tsiku.



wa Mulungu. Alaliki, amishonare, aphunzitsi ndi atsogoleri ena sali otsutsana konse ai; iwo onse ali ancito pamodzi "Pakuti tiri ancito anzace a Mulungu." Munthu wina akhoza kucita kanthu kamodzi,ndipo wina akhoza kucita kanthu kena. Comwe wina angacicite ciri cofunika ndi anthu ena onse. Aliyense kufunika kuti mpingo umangike. Otsatira a Yesu asamamenyana wina ndi mnzace. Iwo adzigwirira nchito pamodzi mu nchito ya ikuru ya kumanga mpingo. Ndi cinthu cacisoni kwambiri kuti nthawi zina tiri nazo zabvuta zonga zimenezi m'mipingo mwathu.

Abusa, amishonare, aphunzitsi ndi atsogoleri ali ofunika kuti akhalepo cifukwa Mulungu amawacititsa iwo kuti agwire nchito yace. Komabe ngakhale ziri tero, si anthuwa omwe amadzetsa mapeto ace ai; ndi Mulungu mwini amene amacurukitsa. Amuna ndi akazi amene akhoza kucita zinthu zosiyanasiyana ndi matalente osiyanasiyana amagwiritsidwa nchito ndi Mulungu. Wina amadzala (amafesa) wina amathirira napalira, koma zinthu zomacokera kwa Mulungu. Ancito aja sapikitsana wina ndi mnzace ai koma kugwilira nchito pamodzi. "Wina aliyense adzalandira malipiro ace kulingana ndi nchito yace yomwe anaicita."

GAWO LACITATU:

Maziko a Mkristu.
(1 Akorinto 3:10-11).

Paulo anali kudera nkhawa kuti afalitse uthenga ku dziko lonse. Iye anali kufuna kufika ku mizinda yambiri ndi maiko ambiri monga akadathera yambiri ndi maiko ambiri monga akadathera. Iye kamodzikamodzi anali kukhalitsa pa malo amoszi kwa nthawi ya itari. Paulo anakhala kwa miezi khumi ndi isanu ndi itatu mu Korinto ndi

zaka zitatu mu Efeso cifukwa ca zifukwa zina za padera za kusowa kwawo. Paulo nthawi zonse anali kuganizira za kunka mtsogolo kukayamba mipingo ina ya tsopano. Iye anali kugwira nchito mukadera kwa kanthawi kocepa, namanga mpingo kapena "kuika maziko". Ndipo nkucokapo kunka patsogolo pamene wasiya ena kuti amange pa maziko amenewa.'

Nthawi ndi nthawi Paulo anazika maziko amodzimodzi Maziko amenewa anali Yesu Kristu. Ndiwo maziko pamene kukula konse kwa Cikristu kuyera kutsamirapo. Kukula kumeneku kuli mu zinthu zitatu:

(1) Kukhululukira - Munthu amazindikira za macimo ace. Ndipo iye amawabvomereza macimowo nalandira cikhululukiro cotheratu. Ndipo pomwepo iye ali ndi cibale ca tsopano ndi Mulungu. Mulungu salinso mdani wace koma bwenzi lace - atate wace.

(2) Mpahmvu za zosowa za tsiku ndi tsiku - Mkristu angalandire kupyolera mwa Mzimu Woyera mphamvu ya zosowa zace. Moyo uli ndi tanthauzo la tsopano ndi colinga catsopano.

(3) Ciyembekezo ca mtsogolo - Mkristu tsopano ali ndi ciyembekezo ca mtsogolo. Mulungu ndiye ciyembekezero cace ndipo Mkristu alibe mantha ndi za mtsogolo, ngakhale pamene ali ndi moyo kapena pamene ali kupenyena ndi imfa.

Kristu ndiye maziko. Iye wa mphumphu Kristu amakwaniritsa zosowa zonse za munthu. Kukula mu Cikristu kuyenera kudza kucokera kwa Mulungu.



M'moyo watsopanowu mtundu wathu, khungu lathu, maphunziro athu, kapena malo omwe tiri nao pakata pa anzathu ziribe kanthu. Zinthu zoterezi sidzitanthauza kanthu konse. Kuti munthu ali naye Kristu ndizo zomwe zifunika ndipo iye ali woperekа kwa onse mofanana.

Pakati tidasankhidwa ndi Mulungu yemwe anatipatsa ife moyo wa tsopano, ndipo cifukwa ca cikondi cace cakuya ndi cisamaliro cace ca pa ife, tiyenera kumacita zokoma mtima ndi cofatsa kwa ena. Tidzikhala aulemu ndi okonzeka kukhululukira. Kumbukirani kuti Ambuye anatikhululukira ife, coteronso tiyenera kukhululukira ena. Koposa zonse tiyenera kulola cikondi kutsogolera miyoyo yathu cifukwa potero mpingo wonse udzakhala pamodzi mwa mvano ndi ngwiro.

Tidzilola mtendere wa Kristu kulamulira mitima yathu ndi miyoyo yathu, pakuti iyi ndiyo nchito yathu ndi mwai wathu monga ziwalo za thupi lace.

GAWO LACINAI:
Akristu - Osankhika Ace.

Osankhika ace a Mulungu ndiwo amene apereka mitima yao ndi myoyo yao kwa Yesu Kristu. Okhulupirira ali "Oyera" ndi "okondedwa" ndi Mulungu. Iwo sali angwiro, koma lai oyera pamaso pa Mulungu ndipo kukhala oyera idayenera kukhala "mbendera" yathu m'moyo. Osankhidwa ali okondedwa a Mulungu; iwo ali ana ace ndipo ali matengo wapatari pa maso pace.

Cipiriro ndi cidziwitso zidayenera kumagwiritsidwa nchito ndi onse okhulupirira mwa Kristu. Akristu adzionetsera cifundo ndi cidziwitso.

mtendere m'mitima mwathu. Iye adzatipatsa cidziwitso ndi cipiriro ngakhale pamene zinthu zaipa.

Ife tiyenera "kumakondwera mwa Ambuye nthawi zonse." Paulo anali mu ndende koma anagwiritsa nchito liu lakuti cimwemwe kawiri ndi kawiri. Iye anakondwera kuti Ambuye anampatsa moyo wa tsopano mwa Kristu Yesu. Ici cinampatsa cimwemwe conse ndi cifukwa comwe iye anali kukhalira moyo Mkristu amene akondweradi mwa Ambuye alibe nthawi ya kutaya kumacita mkangano wopanda pace.

"Kufatsa kwanu kuzindikirike ndi anthu onse." Kufatsa kutanthauza cidziwitso, kukhala munthu waciweruzo cabwino ndi kukhala wolola kuona anthu ena kukhala ndi malo ena. Nthawi zambiri Akristu sawa mvesetsa ndiponso amanyodoledwa, koma ife tidzikhalabe opirira ndi okoma mtima. Pamene ticita izi tiri mboni ku cisomo ndi ukoma wa Mulungu. Tiyenera kuonetsera kugatsa kwathu, osati modzitukumula koma modzicepetsa mwa mzimu wa Kristu.

GAWO LACITATU:

Pamene Mtendere wa Mulungu Ulamulira Miyoyo Yathu.
(Akolose 3:12-15).

Paulo atiuza akuti tisiye kotheratu moyo wathu wa kale wa ucimo ndi kutenga moyo wa tsopano mwa Yesu. Monga Mkristu uli kukhala moyo wina wa tsopano womwe uli kuphunzira zina ndi zina zambiri za zomwe ziri zabwino, ndi kuyesetsa kukhala monga Yesu Kristu yemwe analenga moyo wa tsopano mwa inu.



GAWO LACINAI:

Tiyenera Kufa Kuti Tikule.
(2 Akorinto 5:14-17).

"Cifukwa cikondi ca Kristu citikakamiza ife." Paulotu kuti adzisamalira kwambiri za Akristu zinadza cifukwa kucokera mu cikondi cacikuru comwe Kristu anali naco pa iye. Cikondi cacikuru cimeneci cidampanga kuti akhale ndi cilakolako cacikuru ndi kumanganizira Akristu amenewa ndipo izi zidampanga kuti asadzitamandire ndi kunyada. Paulo anali wodzicepetsa. Iye anatsimikiza kuti Kristu anadera anthu onse. Coonadi cimeneci ndico cinalamulira maganizo ace ndimoyo wace wa Paulo.

Pamene tilandira Kristu monga Mpulumutsi wathu timacokera mu imfa kunka ku moyo Iye. Amene samdziwa Kristu zoonadi ali wakufa, koma mwa cikhulupiriro mwa iye munthu amacoka ku imfa kunka ku moyo wosatha. Pokhapo pamene munthu wafa mwa iye yekha ndipo pamene iye angathe kukhala moyo wa Kristu woonadi.

MTSOGOLERI:

Pamene taika maziko a Kristu m'miyoyo yathu zinthu zazikuru zikhoza kucitika mu Dzina lace. Mkristu aliyense woona ali ndi maziko ace mwa Kristu. Koma kawirikawiri timalola satana kudza m'myoyo yathu ndipo ife timakhala ozizira ndi osasinthika ndi osasamala. Sitiwerenga Zipangano zathu (ma Baibulo) ndi kupemphera tsiku ndi tsiku, sitipita kumapephero ku calici kawirikawiri. Zinthu zimenezi zimatipanga kukhala ofooka monga Akristu.

Kristu ndiye maziko a Kukula konse mwa Cikristu. Pamene maziko amenewa alimba pomwepono tiyembekezedwa kuti tidzikula.

PHUNZIRO 2

KUPITIRIZA KWATHU KWA KUMVERA KRISTU

Nthawi yathu ndi Mulungu:

Nyimbo ya Azimai ndi vesi:

Vesi loloweza: *"Ndilondetsa polekezerapo, kutsatira mfupo wa maitanidwe akumwamba a Mulungu a mwa Kristu Yesu."*
*Afilipi 3 :14.*

Lemba lowerenga: Afilipi 3:7-16.
Akolose 3:1-3.

Pemphero:

MTSOGOLERI:

Kawirikawiri tizidzifunsa tokha funso ili. Kodi cifukwa cakukhalira ine moyo nciani?

Anthu ambiri amamvera ngati kuti pamene iwo amulandira Kristu afika ku mbendera yomariza ya moyo wao. Iwo amamvera kuti pamene amulandira Kristu ndi kubatizidwa alino bwino. Izi siziri zoona konse ai - kumulandira Kristu ndi kuyambirira cabe kwa kukhala moyo wodzala ndi cuma mu cifuniro ca Mulungu.

Lero tidzaphunzira momwe tingakulire monga Akristu.

GAWO LOYAMBA:
Kusankha mbendera ya Moyo Wanu Wa Cikristu.
(Afilipi 3:7-11).

Pa mseu wopita ku Samasiko, Paulo anali ndi cisankho cacikuru. Iye anayenera



GAWO LOYAMBA:
Pamene Akristu Samvana.
(Afilipi 4:1-3).

Paulo anakhazikitsa mpingo ku Filipi. Anthu akomweko anamkonda Paulo kwambiri. Ndipo cotero iwo anatumiza m'modzi wa iwo kuti akonetse cikondi cao kwa Paulo pamene anali mu ndende ku Rome. Paulo anayankha polemba kalatayu kwa Afilipi.

Paulo anakonda mipingo yace yonse, koma palibe wina womwe anaukonda koposa uwu wa ku Filipi. Paulo anawauza iwo kuti inu "Muli cimwemwe canga" cifukwa cikumbukiro cao onse cinadzetsa cimwemwe mu mtima mwace. Iye anawachanso kuti "korona" wace kuonetsanso kunyadira kwace kwa iwo. Tikhulupirira kuti anali ndi ciyanjano codabwitsa ndi anthu amenewa.

Ngakhale mu mpingo wa bwino wa ku Filipi, kusamvana kunauka. Akazi awiri, Euodiya ndi Suntuke, anakangana. Iwo onse anali abwenzi a Paulo ndipo iye anamva cisoni cifukwa cakusamvanako. Ndipo Paulo anawadandaulira iwo kuti athe kusamvana kwawoko "mwa Ambuye". Mwa cisoni zinthu zoterezi zimaoneka pakati pa Akristu, koma Paulo akuti, "Koma zisatero ai."

Akazi amenewa omwe anali ancito okhulupirika anagwira nchito dzanja ndi dzanja ndi Paulo. Iwo anaonetsera mtengo wao monga Akristu. Kusamvana kunali kuonetsa momwe iwo analira ndi mpingonso.

GAWO LACIWIRI:
Pamene Mtendere Wa Mulungu Utitsogolera.
(Afilipi 4:4-7).

Ngati tilola Mulungu kuti akhale mtsogoleri wa miyoyo yathu iye adzasunga

## PHUNZIRO 11

## KUKULA M'CIDZIWITSO NDI CIPIRIRO

Nthawi yathu ndi Mulungu:

Nyimbo ya Azimai ndi vesi:

Vesi loloweza: *"Koma tisaleme paku-cita zabwino; pakuti pa nyengo yace tidzatuta tikapanda kufooka."*
*Agalatiya 6:9.*

Lemba lowerenga: Afilipi 4:1-7.
Akolose 3:12-15.

Pemphero:

MTSOGOLERI:

Lero tidzaphunzira za cidziwitso ndi cipiriro. Izi ndi ziwiri za zofunikira zobvuta kwambiri za Mkristu kuti akhale nazo, koma ndizo ziwiri za zofunikira koposa kuti Mkristu akhale nazo.

Ndi nthawi zingati timamva azimuna ali kunena, "Mkazi wanga sandimvetsa bwino." Kapena mkazi amati "Mwamuna wanga sandimvetsa bwino." Acinyamatanso nao amatero kunena za makolo ao. Mungakhale ziwalo zambiri mu mpingo mwanu omwe amadandaula kuti wina amvetse za iwo. Phunziro lathu la lero lidzatithandiza kuzindikira kwace kwa cidziwitsi ndi cipiriro, ndi kuona kuti kodi tingakule bwanji mu zofunikira za Cikristu.



kusankha kukhala mtsogoleri ndi wolamulira wa mtundu wa Ciyuda ndi kusankha kutsatira Yesu Kristu. Paulo anali m'Yuda pakati pa Ayuda. Iye anali m'Yuda pakubadwa. Ndipo anafikiza pa mbendera ya munthu wa Ciyuda aliyense. Iye anasunga malamulo onse. Ndipo Paulo anali wonyadira cifukwa ca zomwe adazicita monga m'Yuda.

Ndipo tsiku lina Kristu anadza m'moyo wace. Paulo anena kuti pamene Kristu analowa m'moyo wace anazindikira kuti zinthu zonse zomwe anali kuziganizira ndi kuti zinali zofunika kwambiri zinali zacabe. Paulo anayamba kuzindikira kuti zinthu zonse zomwe zinali kuoneka kuti zinali zopambana m'moyo wace zikadaononga moyo wace.

Paulo anazindikira kuti iye anasowa Kristu koposa kanthu kena kali konse. Ndipo cptero, iye anasiya zinthu zonse za m'moyo wace wa kale, ndi kulandira Kristu monga Mpulumutsi wace.

Pamene Paulo anali mu ndende iye anayang'ana moyo wace wonse monga Mkristu. Panali zaka zambiri za mabvuto ndi mazunzo cifukwa ca Kristu, koma mabvuto onsewa adampangitsa Paulo kudziwa kuti adasankha cisankho ca nzeru.

Lero, ngati mutaitanidwa kuti mukazunzike cifukwa ca Kristu, kodi mudzakhala olimba kwakuti mudzatha kuima pa muimira coona mu dzina la Yesu Kristu kapena cikadakhala cofewa kuti mukhonjetsedwe ndi kuti Satana atenge ndi kuulamulira moyo wanu.

Aliponso awo amene ali olola kuti abvutike mabvuto a m'thupi mwao cifukwa ca kristu,koma sangathe kupeza mphamvu zakuti akhale moyo wa Cikristu tsiku ndi tsiku.

Tiyeni tipemphere kuti tidzakhala olola kusauka kapena kukhala moyo wa Cikristu tsiku ndi tsiku. Tiyeni tidaikhala olola kucita kanthu kali konse komwe atiitana kuti tikacite.

GAWO LACIWIRI:

Kupitirirabe Kukula.
(Afilipi 3:12-16).

Paulo anali ndi cilakolako cacikuru ndithu cakuti akhale wa ngwiro mwa Kristu, koma iye anazindikira kuti sanatha kukhala wa ngwiro. Pamene tikhala cifupifupi ndi Kristu ndipomwe timazindikira kuti sitiri anthu a ngwiro.

Paulo atiuza kuti ngakhale iye sali wa ngwiro ali kumagwirabe nchito yakuti akhale wa ngwiro mwa Kristu. Koposa zinthu zonse Paulo anafunitsa kuti adziyese muyeso womwe Mbuye wace anali kuyembekeza kuti iye aufike. Iye sanatha kuti agwiritse mwala Mpulumutsi wace yemwe adacita zambiri kwa iye.

Paulo anali kuopa kuti ziwalo zina za mpingo wa ku Filipi anali kuganiza kuti anakhala "angwiro". Paulo anafuna kuwathandiza iwo kuti azindikire kuti sanakhale angwiro. Iye analimbikitsa iwo kuti apitirire kunka ku mbendera ya mphoto ya kuitana kwa pamwamba kwa Mulungu mwa Kristu Yesu.

GAWO LACITATU:

Kufunafuna Zinthu Zakumwamba.
(Akolose 3:1-4).

M'macesi amenewa Paulo atikumbutsa kuti "tinaleleredwa ndi Kristu." Ubatizo ndi cisonyezo ca kufa kwathu kwa moyo



MTSOGOLERI:

Tiyeni titenge nthawi ya pemphero la padera. Funsani mzimai aliyense apemphere kufunsa Mulungu kuti atithandize wina ali yense wa ife kugonjetsa mayesero omwe adza kwa ife. Tifunse mphamvu ndi cidziwitso kuti tidzikhala moyo wa Ambuye wathu tsiku ndi tsiku.

Paulo anenera kuti palibe yesero lomwe iidza kwa inu limene silinadza kwa mwamuna ndi mkazi wina aliyense. Tizizindikira kuti ena onse anaonanso mayezero otere ndipo kuti iwo anagonjetsa nkhondoyo ya ya Satana ndi kudzikonda.

Mulungu amadziwa pamene tiyesedwa ndipo anaikiratu njira yakuti tipulumukiremo. Njira "imeneyi" ndiyo yakupyolera mwa Yesu Kristu Ambuye wathu. Ngati tiitanira pa dzina lace adzakhala nafe pali ponse pomwe tiyende njira yonse.

GAWO LACINAI:
Njira Zakuzilangila Wekha.
(1 Akorinto 10:23;24;31-33).

Tisamafunafuna ukoma wathu eni ai koma ukoma wa anthu ena. Ici ndico cinali ciphunzitso ca Kristu ndipo Paulo anawakumbutsa Akristu nthawi ndi nthawi. Sicinthu cofewa kuganizira za anthu ena poyamba. Tidziyamba tanganiza za mkazi wathu ndi mwamuna wathu ana athu anazi athu ndi abwenzi athu. Kodi ndi kangati pamene makolo amaiwala ana ao ndi mabanja ao; napita kunja kukacita zokondweretsa za kanthawi zomwe zimasintha kotheratu moyo wao wonse, ndi moyonse wa uja yemwe anakwatirana naye ndi ana ao zonsezi cifukwa ca ka nthawi ka zonkondweretsa kadyera kace.

Akristu ambiri sanazindikire nchito yao ya kulemekeza Mulungu m'moyo wa tsiku ndi tsiku. Iyi ndi nchito yathu. Ici cicita kuposa kupereka umboni ndi kuyimba zinyimbo za kuyamika kwa Mulungu. Moyo wonse uli wopatulika, ndipo moyo wathu wakudzicepetsa wa tsiku ndi tsiku uyenera kukhala wodzipereka ku ulemerero wa Mulungu.



wakale, pamene tiri kumizidwa" m'madzi. Kuuka kumaonetseredwa pamene tiuka kuyenda m'moyo wa tsopano. Pamenepo, ife, monga Akristu ku mbali ina ya manda; tiri kuyenda ndi Kristu.

Tsopano tiri mbadwa za ufumu wa Mulungu, ndipo maganizo athu onse ndi zofuna zathu zonse ziyenera kukhala mwa Kristu.

Paulo atikumbutsa kuti pamene tikhala Akristu tiri akufa ku moyo wathu wa kale wa ucimo, koma tiri a moyo mwa Kristu Yesu. Ife tiri mwa Kristu amene ali Mulungu, ndipo palibe wina aliyense yemwe angatilekanitse kucoka ku cikondi ca Mulungu mwa Kristu Yesu.

GAWO LACINAI:
Mapeto ace Akukula Mwa Cikristu.

Paulo anakhulupirira kuti tidzikhala nayo mbendera ya moyo wathu. Munthu pena sangafike mbendera yace koma ncootheka kuti munthuyu sadzapita pamwamba kuposa mbenderayo.

Paulo anasankha mbendera yoposa zonse ya moyo wace. Izi zinali tero kuti am'dziwe Kristu mwa thunthu. Kodi titanthauzanji ponena kuti kumdziwa Kristu? Ena anamva za Kristu koma sadampanga kukhala mbali ya moyo'wao. Pena citsanzo ici cidzathu kutithandiza kumvesetsa. Munthu asankwatirane ndi mkazi amayamba wadziwa zina za mkazi uja. Iye anamva za kukongola kwa mkaziyo, nzeru zace, momwe anali kucitira maphunziro ace ku sukulu, mkhalidwe wace, moyo wace wa pabanja, ndi makolo ace kuti ngotani. Ndipo akatero amakwatira mtsikanayo namkonda. Tsopano cimatsatirano ndi ukwati wa cuma, wolemerera ndi womwe

uli ndi tanthauzo lace lenileni la ukwati. Cikondi cimasefukira kwa ana. Kupyolera m'misozi ndi zisangalalo (phwete), kupyolera mu cimwemwe ndi cisoni, amayenda ndi kugwada mu pamphero onse pamodzi. Tsopano mwamuna amam'dziwa mkazi wace - miyoyo yao yakhala umodzi. Ngakhale tero miyoyo yathu iyenera kukhala ndi Kristu.

MTSOGOLERI:

Paulo atiuza ife ngati tifuna kuti tipambane m'miyoyo yathu ya Cikristu tienera m'miyoyo yathu. Ngati sititero ambiri a ife tidzalephera m'moyo wa Cikristu monga momwe anthu ambiri amalephera ngati ana ophunzira. Iwo ali ndi zinthu zambiri zomwe zifuna nthawi yao ndi kuti adzicite. Lero kodi muli olola kucotsa zinthu zonsezi zomwe zikuletsani kuti mutumikire Kristu kucokera m'moyo mwanu?



sitidziwa kusewera sewero la moyo ngati sitifika ku calici komwe timaphunzira kutumikira Ambuye wathu.

7. Mvetserani kwa wophunzitsa - wamasewera adzakhala wopanda pance ngati akana kumvera wophunzitsa ndi kutsatira malamuli ace. Comweconso tiri opanda pace kwa Ambuye wathu ndi Mpulumutsi wathu Yesu Kristu ngati tilephera kumtsatira ndi kukhala monga mwa malamulo ace.

GAWO LACITATU:
Cilango M'mayesero.
(1 Akorinto 10:12-13).

Akristu a ku Korinto anayesedwa koopsa, makamaka mu zigololo. Mzindawo unadziwika ndi cigololo comwe cinalimo ndipo cinali capafupi kwa Akristu kumeneko kutsatira zomwe zinali kucitidwa ndi anthu ambiri. Ndiponso anayesedwa kupembedza mafano. Ziwalo zina za mpingo zinali kumatsikiza kuti iwo ali otetezeka kotero kuti sanayenera kuopa mayeserowo konse ao. Koma Paulo anaona ngozi yace ya kutsimikiza kotereko, ndipo anawakakamiza kuti akhale ocenjera, akhale osamalira ndi odzilonda okha. Ife tonse tidziwa anthu ena abwino omwe anagwidwa ali osazilonda okha ndipo anthuwa adzetsa manyazi ku dzina la Kristu.

Pamene Mulungu aloleza mayesero, sikuti afuna kuti Mkristu agwe, koma kumuyesa. Mu kuyesedwa kwace angakule ndi kukhala Mkristu wolimba. Pamene Mkristu agonjetsa mayesero amadziwa mphamvu za tsopano ndi kutsimikiza mtima.

Kawirikawiri timaona kuti mayesero ali osiyana ndipono ndi kuti palibe munthu wina aliyense anawaona poyamba. M'mene

3. Maswiiti amapanga anthu amasewera kukhala aphuma - amangothamaga mtunda wocepa ndipono basi sangathe kupitilirapo. Maswiiti saletsedwa pakati pa Akristu, komatu iwo amatipangitsa ena a ife kukhala onenepa kwambiri ndi ena kukhala ndi mano oola. Tiuzidwa kuti sunga alibe cakudya cothandiza thupi kwenikweni ai.

4. Kudya katatu patsiku - ambiri a ife tidziwa kufunika kwace kwa cakudya cabwino ku makhalidwe a matupi athu. Sikwa matupi athu okha ai komanso maganizo athu. Nzeru zamakono zitiphunzitsa kuti mwana amene akula wopanda cakudya cabwino ceniceni sadzakhala ndi maganizo abwino monga momwe akadazitira ngati akadapatsidwa cakudya coyenera. Ngati tiri amphamvu m'maganizo ndi m'thupi tidzatumikira Ambuye wathu bwino.

5. Kugona pa nthawi ya 9 koloko - lamulo limeneli lingagwire nchito kwa Mkristu mu njira ziwiri. Poyamba, kwa munthu wacikulire; ngati mwamuna acoka panyumba pace nthawi ya usiku kunka ku makondwerero ndi akazi ena - amaononga banja lace ndi nyumba yace - osati moyo wace wokha ai komanso ao amene ali cifupifupi naye. Monga momwe wa masewera amaononga thupi lace pamene salisamalira ndi kusamapumula, comweconso munthu amaononga banja lace pamene salisamalira. Kulionga cifukwa ca makondwerero a kanthawi kosepa basi! Kodi zikondwerero zimenezi zimakhaladi zikondwerero pamene ziri kuswa malamulo a Mulungu, ndi cikumbumtima cathu.

6. Kumakhalako pokonzekera nthawi zonse - kodi ife monga Akristu tingatumikire bwanji Ambuye wathu ngati tilephera kufika ku calici komwe tingaphunzitsidwe. Ife



PHUNZIRO 3

Nthawi yathu ndi Mulungu:

Nyimbo wa Azimai ndi vesi:

Vesi loloweza: *"Iye wakulakika adzalandira izi; ndipo ndidzakhala Mulungu wace, ndi iye adzakhala mwana wamga." Cibvumbulutso 21:7.*

Lemba lowerenga: Aroma 7:13-25.

Pemphero:

MTSOGOLERI:

Kawirikawiri Akristu a tsopano amafunsa, "Kodi n'capafupi kukhala Mkristu? Yankho loonadi ndilo lakuti, "Iai, sicofewa kukhala Mkristu weniweni." Tisama soceretsa ana kapena anyamata pomawauza kuti ndi cinthu cofewa kukhala Akristu.

Ndi cinthu cobvuta kuti mukhale Akristu odzipereka. Nthawi ndi nthawi mumayesedwa. Pali zobvuta zomwe nthawi ndi nthawi zimadza kwa ife. Ucimo nthawi zonse uli pamaso pathu. Lero tidzaphunzira momwe mabvuto amenewa ndi mayesero amenewa angatithandizire kukula monga Akristu.

GAWO LOYAMBA:
Kodi Lamulo Liri Ndi Nchito Zotani pa Mkristu? (Aroma 7:1-12).

M'mavesi amenewa Paulo ali kuyesa kutionetsa kuti Malamulo a Mose ali ndi malo otani m'moyo yanthu monga Akristu.

Kwa mu Yuda, lamulo ndilo linali mbali yopambana ya cipembedzo cace. Paulo analemba nati: Cotero cilamulo ciri coyera, ndi cilangizo cace ncoyera, ndi cilungamo, ndi cabwino. Koma kodi lamuloli limatani kwa Mkristu?

Akristu a Ciyuda anali kuganiza kuti kukhala Mkristu sikunasinthe coonadi cakuti iwo anali omangika kucilamulo. Ku mbali ina kunali ao omwe anali kuganiza kuti kukhala Akristu iwo anali kumasuka kuti akhoza kumacita zina ciri zonse iwo anafuma kuti adzicite.

Cilamulo cimatithandiza ife kumadziwa pakati pa cabwino ndi coipa. Cotero lamulo limationetsa ife kuti tiri otayika mu ucimo. Pamene tiphunzira cilamulo tinazindikira kuti ciri cosatheka kucisunga. Sitingathe kukhala angwiro monga momwe Mulungu afunira kuti tikhale angwiro; ndipo cotero, tiyenera kutebenukira kwa Iye yekha amene ali wangwiro ndi wabwino Mwana wa Mulungu. Iye angacotse ucimo mwa ife m'myoyo yathu ndi kutipanga kukhala olandirika pamaso pa Mulungu.

GAWO LACIWIRI:
Tidzilimbika kuti Titumikire Mulungu.
(Aroma 7:13-23).

Paulo atiuza kuti kuyambira pa nthawi imene tapulumutsidwa tidzakomana ndi zobvuta. Paulo ndiye anali mmodzi wa Akristu akuru ndithu omwe anakhalako; koma ngakhale zinali tero anali kuyesedwa kuti acimwe.

Paulo anati, "Sindikhoza kumvesetsa nchito za ine mwini. Pakuti sindicita zimene ndifuna kuti ndicite,koma ndimacita



2. Ngati anali kudya ma swiiti adzakhala wa phuma. Sadzatha kusewera masewera bwino ndipo sadzatha kusewera nao mpaka kumapeto amasewerawo.

3. Ngati sanadya cakudya coyenera sadzakhala wa mphamvu kokwanira kusewera mazewera wo.

4. Ngati sanagone msanga pa nthawi ya usiku adzakhala wotopa kusewera masewera aja.

5. Ngati sanacita nao pa nthawi zonse zakukonzekera sazadziwa momwe angasewerere masewerawo.

GAWO LACIWIRI:
Yerekezani Wamasewera Ndi Mkristu.

Cifukwa ciani Paulo anayerekeza wa masewera ndi Mkristu? Tiyeni tiyang'anenso za malamulo asanu ndi awiri aja a anthu amasewera ndi kuwacititsa mu moyo wa Cikristu.

1. Pamene munthu amwa mowa samaononga moyo wace iye mwini ai komanso miyoyo ya banja lace ndi okondedwa ace. Anthu ambiri amayamba ndi kumwa kabotolo kamodzi kamowa, ndipo posacedwa mayamba kufuna kumwako kufikira miyoyo yao yonse yakhala pa cikopo ca mowa basi. Miyoyo yao iri yopanda pace cikopo ca mowa cawagwira kotheratu kotero kuti satha kucileka.

2. Osakoka fodya osati kukoka ndi khalidwe cabe loipa ai lakuti sukhala Mkristu koma kuti mzaka za makonozi caoneka kuti ncoonadi kuti kukoka fodya kumadzetsa imfa ndi maudwale kwa anthu ambiri. Ndiponso, ndi khalifwe loipa lomwe liri lobvuta kulisiya.

Paulo anali kufuna kuti iwo adzuke ndi kuti akhale naco cilakolako cakugwira nchito ndi kukopa otayika. Kukhala moyo wa Cikristu ndi nkhondo ndipo ife monga Akristu tiri asilikari a Kristu.

Paulo anadziwa kuti kuphunzitsidwa kunali kofunikira kwa Mkristu monga momwe kulira kwa munthu wamasewera (wamaliwiro). Pamene tinali ku sukulu lapamwamba anyamata omwe anali kumenya mpira anali kupatsidwa malamulo ena. Malamulo amenewa anali otere:

1. Osamwa mowa kapena zina zolezeretsa.

2. Osakoka fodya.

3. Osadya ma siiti.

4. Adzidya zakudya zabwino katatu pa tsiku.

5. Adzipezeka alipo madzulo ali onse pa nthawi ya 9 koloko.

6. Adzipezeka aliko kukukonzekera mpira tsiku ndi tsiku.

7. Nthawi zonse adzimvetsera kwa wowaphunzitsa uja.

Ngati wina wa anyamata aja anaswa limodzi la malamulo amenewa anali kucotsedwamo mu gululo. Cifukwa ninji?

1. Ngati mnyamata uja amwa mowa sadzakhoza kukhala wocenjera m'maganizo mwace. Ndiponso kumwa mowa kamaononga thupi.



zinthu zomwe sindifuna kuti ndidzicite." Ndi kangati pamene timadziwa kuti ici ncoipa ndi kunena kuti cinthuci ncolakwika ndi coipa; komabe, mu kamphindi kocepa ka kufooka tidzipeza tokha tiri kucita cinthu comwe cija tinadana naco?

Akristu ena angayesedwe kuti amwe mowa. Abwenzi ao angawaseke ndi kuwanyodola ngati iwo akana kumwa mowawo. Anyamata ndi atsikana amayededwa kucita cigololo pa kanthawi kakufooka. Malo owerengeka mu dziko lomwe atsikana ali aufulu kudzipereka okha ndi kukhala a mtendo wa ukuru ku ulipira. Muno mu Zambia ngati mtsikana akhala ndi mwana asanakwatiwe palibe mwamuna woyenera yemwe angadzamukwatire. Komabe timaona kuti mwina maukwati amacitika cifukwa mtsikana ali ndi mimba.

Palinso, yesero lakufuna kunyenga msukulu nthawi ndi nthawi ndi mu malonda. Kawirikawiri asikolala ndi anthu ambizinesi amaganiza kuti ayenera kunyengapo cifukwa "wina aliyense amatero." Mkristu wa nchito lero amayesedwa kawirikawiri kutaya nthaiw mu njira ya kuti safuna kuti patsikulo agwire nchito monkwanira ndi ndarama zomwe amalandira. Ngati ife tileka kulankhulapo pamene tiona kuti cinthu cosalungama ciri kucitidwa tilakwa. Izi ndi njira zina zomwe Akristu amayesedwera. Ucimo nthawi zonse uli ndi ife.

Kodi tingamakomane nayo bwanji nkhondo ya kulimbana ndi ucimoyi nthawi ndi nthawi?

GAWO LACITATU:

Njira ya Kucigonjetso.
(Aroma 7:24-25).

Paulo anadziwa kuti panali "njira" yomwe tingapambanire ucimo. "Njirayi" inaperekedwa ndi Mulungu kupyolera mwa Yesu Kristu Ambuye wathu. Pamene tiyesedwa iye ali wokonzeka nthawi zonse kutithandiza ife ngati tiri olola kuitanira pa iye.

Monga Akristu tiyenera nthawi zonse kumakhala ocenjera ndi ucimo. Ucimo nthawi zonse umakhala ukali kulindilirira ife pa nthawi zathu za kufooka.

Monga Akristu tidzipemphera ngati tifuna kuti tipambane ucimo. Pamene tiyesedwa tidziitanira pa dzina la Ambuye; iye adzatipatsa mphamvu zomwe tisowa kupambana mayeserowo.

Anthu ambiri amati Akristu sadayenera kumapezana ndi mayesero ndi zobvuta m'moyo. Kodi izi zingatheke bwanji ngati Ambuye wathu weni anayesedwa. Tisamayesera kuti mabvutowa ndi mayeserowa kuti ndi zinthu zomwe ziri zosatheka kudzipambana koma tizimvesetsa kuti zinthuzi zimacita zinthu zina m'miyoyo yathu. Sitingakule monga Akristu ngati tiribe nthawi izi za mayesero. Zinthu zoterezi zimatipanga kukhala Akristu olimba ndi okhazikika.

Munthu amene amasewera mpira wa citanyu (wamiendo) sangakhale munthu wodziwa kumenya mpirawo ngati iye angomyetsera ku malangizo cabe ocokera kwa uja amamphunzitsa uja iai. Iye ayenera kulowa m'masewerawo, nakomana naye wolimbana nayeyo mbwalomo, ndikuti aciteko tizironda. Kulowatu



PHUNZIRO 10

KUKULA M'KUDZILANGA WEKHA

Nthawi yathu ndi Mulungu:

Nyimbo ya Azimai ndi vesi:

Vesi loloweza: *"Cilango ciri conse, pakucitika, sicimveka cokondweretsa, komatu cowawa; koma citatha, cipereka cipatso ca mtendere, kwa iwo ozoloweretsedwa naco."*
*Ahebri 12:11.*

Lemba lowerenga: 1 Akorinto 9:24-27.
1 Akorinto 10:12-13;
23:31-33.

Pemphero:

MTSOGOLERI:

Sicinthu cofewa kukhala Mkristu. Yesu kawirikawiri anauza otsatira ace za mabvuto omwe angapeze pomtsatira Iye. Paulo ndi alembi ena a Cipangano ca Tsopano alozapo, zina za zoopsa zace zakukhala otsatira Kristu. Tiyenera kudzikaniza tokha ndi kuzilanga tokha. Siingakhalenso njira ina.

GAWO LOYAMBA:

Moyo Ufuna Cilango Cawekha.
(1 Akorinto 9:24-27).

Akristu a ku Korinto anagwa mu ulesi wa mzimu ndi kukhala mosasamalira konse. Iwo anali ataya mzimu ndi cikumbu mtima comwe Akristu anayenera kukhala naco.

Mai wace uja anamufunsa nati, "Kodi ukadacita mantha ngati ndikadakhala mawe muno, Maria?"

"Iai, sindingacite mantha," anayankha mwana uja.

Mai uja anayankha, "Kani, sindikhale muno, Maria, sindingamakhale nthawi zonse, koma Ambuye ali nawe nathwi zonse. Adzakhala nawe, ngakhale nyali zizime."

Mariya sanatha kuyankha mau amenewa ai, koma anayamba kuganiza. Mai wace anacoka mu cipinda muja nyali ija ikali ciyakire; ndipo kwa kanthawi pang'ono anamva kulira kwa koyatsira nyali kalira pamene Maria anali kuzima nyali ija. Ndipo kwa nthawi pang'ono anamva mau a ang'ono mau a citsimikizo akuti, "Tikuoneni Yesu!"

Ici ndico cikhulupiriro.

MTSOGOLERI:

Colinga cace ca moyo ndico kukhala moyo munjira ndi kukhala moyo womwe Mulungu adzakondweretsedwa nao, ndi moyo wathunso. Phunziro lathu likuti kopanda cikhulupiriro sikutheka kumkondweretsa Mulungu. Ndipo cotero, cimo lakusakhulupirira ndi kusakhulupirika ndiwo amodzi a macimo akuru kwambiri.



mbwalo ndi kusewera kumenya mpiraku ndiko komwe kumampangitsa munthu kukhala wosewera.

GAWO LACINAI:

Kulimbana Kwa Ena.

Cipangano cimatiuza za anthu omwe analimbana nazo zobvuta m'miyoyo yao. Inali nthawi ya ora lace la mantha ndi kuti anali yekhayekhapamene Yakobo analimbana naye mngelo nakhala mwana a cifumu ndi Mulungu. Yosefe ndiye anali mwana wokondedwa kwambiri ndi atate wace; pamenepo anatengedwa kunka ku Aigupto kukhala kapoli ndi wa ndende. Yosefe anapambana mabvuto ambirimbiri koma mabvuto amenewa anamthandiza kukhala mwana wolimba wa Mulungu. Ndipo kupyolera mu mphamvu imeneyi iye anatha kumasula abale ace kukhala aufulu. Danieli ndi anzace anaonetsa kulimba mtima kwawo ndi cikhulupiriro cawo pamene anali kukomana ndi dzenje la mikango ndi ng'anjo yoyaka moto. Yohane, mtumwi yemwe Yesu adamkonda, anaikidwa mu ndende pa cilumba capacokhacokha ca Patimo cifukwa ca cikhulupiriro cace mwa Yesu Kristu, koma Mulungu anamdalitsa iye pomupatsa masomphenya akumwamba. Ifenso tidziwa za mabvuto ndi kulimbana kwace kwa Paulo. Ngakhalenso Ambuye wathu ndi Mpulumutso wathu anauzunzika pa mtanda kuti inu ndi ine tikhale nawo moyo wosatha.

MTSOGOLERI:

Sitinenatu kuti wina adzipitapita kukafunafuna mbavuto iai, koma pamene tipezana zaowo mabvutowo tiyenera kumakomana nao mwa mphamvu ya Ambuye wathu Mpulumutsi.

Tidzikumbukira kuti tingakule monga Akristu kupyolera mu mabvuto a m'moyo.

## PHUNZIRO 4

### AKRISTU AMAKULA KUPYOLERA MUKUPHUNZIRA

Nthawi yathu ndi Mulungu:

Nyimbo ya Azimai ndi vesi:

Vesi loloweza: *"Pakuti zonse zinalembedwa kale zinalembedwa kutilangiza, kuti mwa cipiriro ndi citonthozo ca malemba, tikhale ndi ciyembekezo."*
*Aroma 15:4.*

Lemba lowerenga: Macitidwe 17:10-12.
2 Timoteo 3:10-17.

Pemphero:

MTSOGOLERI:

Pamene tipita ku sukulu, amatipatsa mabuku;sukulu lingakhale losatheka kukhala lopanda mabuku. Palibe munthu yemwe angakhale loya popanda ciyambi ceniceni codziwa Malamulo; palibe munthu anganene kuti adziwa sayansi (zofufuzafufuza) ngati iye sadziwa ziyambi ndi zoona zace za sayansi. Ndipo palibe Mkristu yemwe ali wa mtengo wace monga Mkristu wopanda ciyambi ceniceni, ndi nzeru za kudziwa Cipangano (Buku Lopatulika).

GAWO LOYAMBA:
Tidzimvera Zoonadi zace za Mulungu.
(Macitidwe 17:10-12).

Paulo anacoka ku Tesalonika cifukwa ca cizunzo coopsa comwe cinali kumeneko.



Cipulumutso ndi mphatso yocokera kwa Mulungu. Ife palibe comwe tacicita kuti ticipeze cipulumutsoco. Cipangano citiuza kuti mwa cisomo kupyolera mu cikhulupiriro mwapulumutsidwa inu osati kwa inu nokha koma ndi mphatso ya Mulungu.

Cikhulupiriro mwa Yesu Kristu monga Mbuye ndi Mpulumutsi zimatitengera ife cipulumutso, komatu cikhulupiriro cisathere pokhapo ai. Cikhulupiriro ciri cofunika tsiku ndi tsiku la moyo wathu ndipo cikhulupiriro cathu ciyenera kupitirira kukula kuyambira pa tsiku lija tinapulumutsidwa. Cikhulupiriro cimeneci cidzatuthandiza kuthawitsa satana kucoka m'miyoyo yathu ya tsiku ndi tsiku.

GAWO LACINAI:
Kodi Cikhulupiriro Cimakula Bwanji?

Ngati munthu akana kulandira Kristu cifukwa cakuti cikhulupiriro cace ciri cacing'ono, nanena kuti adzamulandira pamene cikhulupiriro cace cidzakula, sadzamulandira Kristu ndiponso cikhulupiriro caceco sicidzakula konse. Ndi pomwe pamene tiri kuyamba cikhulupiriro pamene tilandira cikhulupiriro cacikuru. Cikhulupiriro cimakula pamene tikhalira pamodzi ndi anthu a cikhulupiriro. Cikhulupiriro ncopatsirana - cipatsiridwa kucoka kwa munthu mmodzi kunka kwa wina.

Mzimai wina ananena nthano yotereyi kunena za mwana wace wa mkazi, Maria, Maria anali mmodzi wa ana amene amaopa kukagona mu cipinda momwe muli mdima. Iye anali kufuna kuti nyali isamazime usiku wonse. Usiku wina pamene iye anali kulowa m'bulangeti mwace mai wace anadza nadzima nyali, ndipo mwana uja analira kwambiri nati, musadzime nyali mai.

GAWO LACIWIRI:
Cikhulupiriro Cimakula Kupyolera M'cidziwitso.
(Akolose 1:9-14).

Mtsogoleri wa mpingo wa ku Kolose anakacezera Paulo pamene anali mu ndende ku Rome. Iye anamuuza Paulo za mabvuto omwe anali nao mu mpingo. Panali gulu la anthu omwe anali kumaphunzitsa za bodza mu mpingomo.

Paulo sanacita nao mkangano pa zomwe anali kuganiza, koma anauza anthu kuti aphunzire nafunefune cifuniro ca Mulungu ca kwa iwo eni. Ngati atero pomwepo azadziwa coonadi. Paulo anawauza kuti Mulungu ali zoonadi ndi kuti ngati wina apeza cidziwitso conse ciyenera kudza kucokera kwa Mulungu.

Pamene tikula mu cikhulupiriro ndi cidziwitso pomwepo tikhoza kupilira mu zinthu zonse.

GAWO LACITATU:
Mapeto Ace a Cikhulupiriro.
(Akolose 1:21-23).

Pamene muli cikhulupiriro coonadi mwa Kristu, pomwepo cimadza cipulumutso. Kumbukirani zija zomwe Paulo adamuuza mdindo uja nati "Ukhulupirire Ambuye Yesu Kristu ndipo udzapulumuka." Awa ndiwo mapeto ace akukhulupirira ndi kukhala ndi cikhulupiriro mwa Yesu.

Tisamakaikira mphamvu yace yakuyeretsa ya Yesu Kristu. Tiyenera kunena zikhulupiriro zathu ndi kukhala olola kudziimira zikhulupirirozo ngakhale pa khale zina zobvuta.



Ndipo iye anapitilira nanka ku Bereya komwe anakapita poyamba ku sunagoge wa Ayuda kukalalikira.

Ayuda aku Bereya anamvera bwino uthenga wace wa Paulo ndi mitima yofuna. Iwo anayamba kuphunzira malemba. Iwo anafuna kudziwa ngati zomwe Paulo ndi Sila anali kuphunzirsa zinali zoona. Iwo anali asanamve ndi kale onse mau a Mulungu ali kulalikidwa mu njira yotereyi. Iwo anafuna kudziwa za mbiri za zomwe Paulo anali kuphunzitsa. Ndipo Paulo anali woyamikira kwambiri kuona kuti anthu anali kukondweretsedwa nao mau a Mulungu. Asilaliki athu a masiku ano akadakondwera kwambiri kuona ziwalo za m'mipingo mwao ali kuphunzira Zipangano zao ndi kumaphunzira coonadi eni okha.

Pamene anthu anali kuphunzira ndi kusanthula malembo eni okha ambiri anakhulupirira. Ayuda ndi Amitundu omwe pamodzi, amuna ndi akazi, anakhala otsatira otsatira a Yesu.

Ambiri a atsogoleri athu ndi a mishonare athu anaphunzitsidwa kwa nthawi ya itari ndi mosamalitsa Cipangano. Ici ndi cinthu cabwino. Komabe tiyenera kulimbikitsa nchito ya Akristu ena onse. Akristu ambiri sali osamalira za nchito yao yakuti aphunzire mau a Mulungu.

GAWO LACIWIRI:
Kuphunzira mu Zomwe Zidacitika.
(2 Timoteo 3:10-14).

Timoteo Waciwiri anali kalata wotsiriza yemwe Paulo analemba. Paulo pa nthawiyi ali wokalamba, anali mu nyumba ya ndende mu Rome kuyembekeza kuti aweruzidwe.

Iye anali wodziwa kuti ndithudi adzalamulidwa kuti afe. Ndipo anayamba kumaganiza za bwenzi wace wa cinyamata, Timoteo, yemwe anali mnzace ndi womthandiza kwa zaka zambiri ndipo pa nthawi iyi anali mbusa wa mpingo ku Efeso.

Paulo analibe cilakolako cina conse ca kwa Timoteo coposa cakuti iye apitirire kukula mwa Kristu. Paulo anamuuza iye nati, "pitiriza zomwe udaziphunzira ndi kudzikhulupirira molimbika."

Timoteo anaphunzira kuti kukhala ndi cikhulupiriro mwa Kristu monga Ambuye ndi Mpulumutsi zinali cinai. Cotero, anayenera kupitiriza kukula mu luntha ndi zidziwitso ca Mulungu.

GAWO LACITATU:
Kupeza Moyo Kupyolera M'Malemba.
(2 Timoteo 3:15-17).

Timoteo anakulira mu banja la Mulungu. Mai wace ndi gogo wace anali odzipereka ku Malemba, Cipangano Cakale.

Cipangano citiuza momwe tingakhalire a Akristu. Anthu ambiri analandira Kristu powerenga Cipangano.

Lembali lidauzirudwa ndi Mulungu. Mulungu adauzira kapena kuti anatsogolera "anthu oyera mtima" kulilemba. Ndipo cotero, Cipangano ndi mau a Mulungu.

Lemba limeneli "lipindilitsa mu ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, ndi ciphunzitso ca m'cilungamo."

Lemba ndilo cotitsogolera cathu m'moyo. Tiribenso njira ina yomwe tingadziwire



Pamene muli kutembenuka pa mseu womwe uli kunka kwanu, muona zinthu zambiri zomwe munali kutembenuka pa mseu womwe uli kunka kwanu, muona zinthu zambiri zomwe munali kudziona mukali ana ang'ono. Izi zikukumbutsani kuti muli pafupi ndi kwanu. Inu mudziwa kuti posecedwa mudzafika kwanu komwe kuli a banja lanu. Tsono muyang'ana muona nao atate wamu ndi amai wanu ali nkudza kudzaku lonjerani. Izi ziri monga momwe munali kulotera kuti zidzatero. Cimwemwe ndi cisangalalo cakuti mwafika kwanu kaciwiri! Comweconso ndi Akristu; iwo ali ndi citsimikizo cakuti pamene afika kumapeto a moyo Atate aku mwamba adzakhala ali komweko kukulonjerani ndi kukulandirani.

Ngati tifuna kuti tikhale naco ciyanjano cabwino ndi anthu ena tiyenera kukhala naco cikhulupiriro. Kuti akhale okonwera, mkazi ayenera kukhala naco citsimikizo ca cikhulupiriro ca mkazi wace mwa iye. Mwana nayenso ayenera kumadziwa kuti atate wace amamkhulupirira iye. Ngakhalenso, kopanda cikhulupiriro sitikhoza kumkondweretsa Mulungu. Mulungu sangakondwere naye yemwe amucha iye Atate, koma nasakhala naco cokhukhulupirira mwa iye. Mulungu afuna cikhulupiriro, ndi cikondi ca ana ace.

Ife tiyenera kumalambira Mulungu, koma tisanalambire iye tiyenera kukhala naco cikhulupiriro mwa iye. Tiyenera kukhulupirira kuti Mulungu ndi mlengi wa zinthu zonse ndiponso ndi kuti Mulungu ndiye cikondi.

## PHUNZIRO 9

## KUKULA MUCIKHULUPIRIRO

Nthawi yathu ndi Mulungu:

Nyimbo ya Azimai ndi vesi:

Vesi loloweza: *"Koma cikhulupiriro ndico cikhazikitso ca zinthu zoyembekezeka, ciyesero ca zinthu zosapenyeka."*
*Ahebri 11:1.*

Lemba Lowerenga: Ahebri 11:1-6.
Akolose 1:9-14;
21-23.

Pemphero:

MTSOGOLERI:

Lero tidzapitiriza phunziro lathu la kukula M'cikristu. Kodi cikhulupiriro cingatithandize ife bwanji kukula monga Akristu? Kodi cikhulupiriro nciani? Cikhulupiriro ca Cikristu ndico kukhulupirira mwa munthuyo wocedwa Yesu Kristu, coonadi ca ciphunzitso cace ndi cipulumutso comwe anacitsiriza pa imfa yace pa mtanda.

GAWO LOYAMBA:
Chikhulupiriro Ncofunika.
(Ahebri 11:1-6).

Ngati tifuna kuti tilongosole liu lakuti cikhulupiriro tingatero mu njira iyi: Pena munali mwacoka ku nyumba kwanu ndi ku mako anu kunka kwina kwa zaka zambiri. Ndipo tsiku lina mwaganiza zakubwerera kwanu kukaonana ndi a pa banja lanu.



momwe ndi zomwe tingacite monga Akristu. Cotero ngati tilandira Kristu monga Mpulumutsi wathu tiyenera kumagwiritsa nchito Cipangano monga cotitsogolera cathu. Opanda Cipangano tigakhale monga munthu wopanda miyendo. Munthu wopanda miyendo sangadzithandize kwambiri yekha, banja lace, kapena mnzace. Comweconso ndi Mkristu - ali wopanda nchito kwa iye monga comtsogolera m'moyo wace.

Colinga ca Cipangano ndico kutithandiza kukula monga Akristu.

GAWO LACINAI:
Nzeru Yakuphunzirila.

Kodi cifukwa ninji Akristu amalephera kuphunzira Zipangano zao? Ambiri amati, "Ndiribe nthawi" kapena Ndiribe malo enieni akuti ndingakhalepo ndi kuphunzira." Ena amati, "Sindimvesetsa pamene ndiwerenga Cipangano." Izitu sikanthu koma zowiringula cabe, Satana amakondwera nafe pamene sitiphunzira. Koma pansi pa mtima ifeyo tidziwa kuti tikhoza kuphunzira; tikhoza kuipeza nthawi ngati tifuna kuti titero. Ambiri aife tikhoza kucita zinthu zonse zimene tifuna kuti tidzicite. Mkristu ali yense anayenera kumafuna kuphunzira cipangano cace kotero kuti akhoza kudziwa cifuniro ca Mulungu ca moyo wace wa tsiku ndi tsiku.

Kunali munthu wina yemwe anali wodula ngale (Majewel) yemwe anali kukhala ku dziko la America. Iye nchito yace inali yakumafula miyala ya mtengo wapatari kumaipanga kukhala ngale zokongola koposa ndiza mtengo wapataro.

Usiku wina Yohane anapita ku ofesi wa munthu wodula ngaleyu. Yohane yemwe anali munthu wancito wamba, anaturutsa mthumba mwace kamwala kacabecabe kofiira nakapatsa kwa wodula ngale uja nati, "Ndifuna kuti udule ndi kusalaza mwala uwu." Ndi kuzizwa kwakukuru munthu uja anamfunsa, "Kodi unaupeza kuti mwalawu?" Ndipo Yohane anayankha nati, "Atate wanga anautola ku dziko la Hungary zaka makumi asanu zapitazo. Iwo anaganizira kuti kanali kamwala kokongola. Pamene ndinafika mu dziko lino ndinaupeza uli mu bokosi langa. Wakhala uli m'nyumba zaka zonsezi. Ana anali kuuseweretsa. Mwana wanga wotsiriza anathyolapo dzino lace pa mwala umenewu."

"Usiku wina ndinalota kuti unali mwala wa daimoni womwe uli wa mtengo wa ndarama zambiri, koma suli daimoni ai. Uli wofiira," anatero Yohane. Ndipo wodula miala uja anati, "Iai suli daimoni konse. Ndi mwala winawocedwa ruby." Ndipo Yohane anafunsa nati, "Nanga ngwa mtengo wotani?" Wodula uja anayankha nati, "Ndinganene kuti mtengo wa ndarama zocokera pa K100, 000 - K250,000." Yohane angwidwa ndi nthumazi kotero kuti anatsamira kucitseko.

Ndipo mwala waukuru uja anaufula naupanga ruby ya mtengo wapatari. Ciganizidwa kuti ndiyo ruby yaikuru koposa mu dziko lonse la America kapenanso yokulitsa koposa zonse mu dziko lonse lapansi.

MTSOGOLERI:

Ndi cinthu cacisoni kotani nanga kuti m'mabaja mwina mwambiri Buku lomwe liri la mtengo wapatari woposa ngale zambirimbiri silisamalidwa konse ai ndipo limaganizidwa kuti ndi lopanda pace.



Ndi moyo wotanganidwa ndi nchito, koma wokondwa kwambiri. Moyo womwe uli wa mtengo wace woyenera kukhala nao.

MTSOGOLERI:

Mkazi wa Cikristu amakhala ndi moyo wotanganidwa - kuphika, nthawi zonse kukhala ndi zinthu zonse ziri zaukhondo ndi zokonzekera mwamuna wace pamene ali kucokera ku nchito. Mkazi ndiye ali ndi nchito yoyang'ana panyumba ndi ana. Ndi nchito yodalitsika yotani nanga. Iye ali nayo nchito yakutsogolera ana ace tsiku ndi tsiku mu njira ya Kristu.

Kuphika, kukonza panyumba, ndi kusamalira ana pena zingakhale zosakondweretsa, koma tidzikumbukira kuti palibe njira ina ya ikuru yakutumikira Ambuye wathu ndi ao amene tiwakonda kwambiri. Nthawi imodzi ndinamva Mai Evelyn Mukombo ali kulankhula ndi bwenzi wao. Bwenzi uja anali kulankhula za anzace omwe amaphunzira nao mu klazi lace omwe anapitirira kunka kukaphunzira maphunziro osiyasiyana. Ndipo pamene Mai Evelyn akali khale ndi kamwana kao kaciwiri pa miendo iwo anati, "Komatu taona tiri nao ana athu ndi amuna athu omwe tiyenera kuwakonda cifukwa ngathi athu." Awatu ndi mphatso ya ikuru yocokera kwa Mulungu kwa ife, kodi tingapemphe cinthu cacikuru cotani m'moyo? Uwutu ndiwo moyo wodzala ndi cikondi, cimwemwe ndi ciyembekezo.

Munthu woyambirira kukhala pa dziko lino lapansi iyense anagonjera ku zofuna zace. Iye anadya cipatso coletsedwa ndipo podzikanira anati, "Mkazi yemwe munandipatsa uja; ndiye anandipatsa cipatso ca mu mtengo, ndipo ndinadya." Iyetu anali kunena kwa Mulungu kuti izi ndi zomwe mudazicita Inu; munandipatsa mkaziyu; Mkaziyu anandicimwitsa. Pokanira! Pokanira! Lero tikali kupereka kwa Mulungu zokanira zosayenerazi za ucimo wathu. Ife ticimwa pa - kucita cigololo, kumwa kufikira tasanduka acakolwa kotero kuti sitingathe kugwira nchito konse. Mabanja athu aonongeka ndi miyoyonso ya okondedwa athu. Ndipono pomwepo tiyamba kulira ndi kumati, "Kodi Mulungu wandicitiranji ine zotere?" Mulungu sanadzicita izi konse ai. Moyo wakukhala mu ucimo umapangitsa ciononGeko; osati kwa ife tokha ai komanso kwa ao amene atizungulira ife, ana athu, omwe takwatirana nao, mabanja athu, amaonongeka cifukwa tiri ofooka.

Tsono tiyeni tione moyo wa Mkristu wodzipereka. Ndi zoonadi, koposa kuti iyeyutu sadzakhala wolemera mu mzindamo (m'mudzimo) koma adzakhala mmodzi wa anthu okondwesetsa. Mwamuna wa bwino wa Cikristu amagwira nchito kolimba kuti apeze zothandiza pa banja lace. Iye nthawi zonse amakhala wozazidwa nid cikondi ca ana ace ndi mkazi wace ndi banja lace lonse. Iye amapeza nthawi yakupemphera ndi kuphunzira Cipangano cace pamodzi ndi banja lace. Iye amapita ku misonkhano ya utumiki yonse pamodzi ndi banja lace ku calici. Iye amaganizira za Akristu anzace pamene iwo asowa thandizo lace. Iye sapangitsa mabvuto mu mpingo wace, koma amathandiza kutumikira Mbuye wace mu njira ina iri yonse yomwe angathere. Tayang'anani moyo wace.



Tiyeni tisilire lero lino pamodzi ndi kuphunzira Zipangano zathu tsiku ndi tsiku. Kodi munadziwa kuti ngati muwerenga mitu (macaputa) atatu pa tsiku ndi isanu pa tsiku la mulungu mukhoza kuliwerenga Buku la Cipangano lonse mu caka cimodzi ca thunthu. Tiyeni tipange ici kukhala mbendera yathu ya caka cino.

## PHUNZIRO 5

### AKRISTU AMAKULA KUPYOLERA MU CIYANJANO

Nthawi yathu ndi Mulungu:

Nyimbo ya Azimai ndi vesi:

Vesi loloweza: *"Cifukwa cace tilondole cinthu za mtendere, ndi zinthu zakulimbikitsana wina ndi mnzace."* *Aroma 14:19.*

Lemba lowerenga: Aroma 14:13-21.

Pemphero:

MTSOGOLERI:

Tsiku lina mmodzi wa akulu aboma anafunsa mmodzi wa Akristu athu, "Cifukwa ciani mumapita ku calici kukapemphera ndi kuimba pamodzi pamene mukhoza kutero muli m'nyumba mwanu?" Iwo anali kuimirira pambali pa mbaile. mzimai uja anayankha nati, "Mbuye wokondedwa, lekanitsani malashawa ndipo adzazima nthawi yomweyo, koma taonani kuti apanga moto wabwino koposa pamene ali kuyakira pamodzi onse!"

Lero tiri kupitiriza maphunziro athu akukula kwa Mkristu. Palibe njira yina yabwino ndi yofulumira ya Akristu yakukula yoposa iyi yofunika ya ciyanjano ndi Akristu ena. Munali bvuto loopsa kwambiri pakati pa Akristu mu Rome. Bvuto limeneli linaoopsa ciyanjano ca mu Mpingo.



7. *Cikhulupiriro* - kumakhala okhulupirika ndi odzipereka ku nchito.

8. *Cifatso* - kukhala wodzilamulira wekha, kukhala wolola kudzipereka wekha ku cifuniro ca Mulungu.

9. *Ciletso* - kudzilamulira wekha, kukhala wosaledzera ndi wakukhala nazo nzeru zokhoza kucita zinthu.

Zonsezitu ziyenera kukhala womwe Mkristu ayenera kukhala nazo. Mkristu woonadi "anapacika" kapena kucotsa zonse zilakolako za thupi. Paulo anena kuti ngati mucita izi pomwepono "ciyanjano" ca mpingo sicidzaonongeka.

GAWO LACINAI:

Yerekezani Moyo Waucimo ndi Moyo wa Moyo.

Ndi kangati timamva akunena kuti, "Mulungu anatipatsa zilakolako za thupi; ndipo cotero, tikhoza kucita momwe tifunira eni;" kapena "Mulungu anatipatsa cilakolako cakucimwa ndipo cotero sitifunika kuti tidzidzilamulira zilakolakozi ai." "Mulungu anapanga mowa ndi yinyo; ndipo cotero tiri aufulu kumwa monga tifunira." Izi ndithu ndizo zowiringula zomwe anthu amenena pomakhala moyo wa ucimo. Awatu ndiwo anthu amene akhala moyo wao tsiku ndi tsiku osanganizapo za zomwe zidzacitike mtsogolo mwao pa kufika ku cimariziro za moyo uno womwe akhala mu ucimo.

Pamene tikhala m'moyo wotere wa ucimo wopanga nchito kwa Mulungu wathu kapena anzathu tiona miyoyo iri kuonongeka, mabanja ali kusweka, mitundu iri kuonongeka, ndi cidziwitso comwe ciri kuipsedwa.

14. *Kuledzera* - ucakolwa wakumwa kufikira maganizo ndi thupi zaonongedwa kotheratu.

Izitu ndizotu zofuna za thupi, mapeto akukhala mosayenera. Mapeto a mazimo amenewa ndiwo kuferatu mu mzimu.

GAWO LACITATU:

Cipatso ca Mzimu.
(Agalatiya 5:22-26).

1. Cipatso ca Mzimu ndico *cikondi*. Paulo atanthauza cikondi comwe cifuna zinthu za kumwamba m'moyo, cikondi comwe cimathandiza mnansi, cikondi, comwe cidzafa cifukwa ca abale, cikondi comwe ciri utumiki.

2. *Cimwemwe* - osati kumangokhala nayo nthawi ya kucita masewera ndi zina zosangalatsa moyo, koma cimwemwe cakukhala m'ciyanjano ndi Mulungu.

3. *Mtendere* - osati ufulu wakucoka ku bvuto, koma kukhala naco cikhulupiriro ngakhale pamene mabvuto adza; mtendere womwe uli woposa kuti munthu aumvetse cifukwa uli wa Mulungu. Ndiwo mtendere womwe upambana nzeru zathu.

4. *Kuleza mtima* - kupilira ndi kuona zinthu momwe ziliri, kukhala wokonzekera kufa, inde monga Kristu anafa, ngati tingatero.

5. *Cifundo* - Mkristu ali, coyamba, nthawi zonse munthu wokhazikika. Iye sacita zinthu mwa ukali ndi mphamvu kapena kupweteka ena. Iye amatsogozedwa ndi cikondi mu zinthu zonse zomwe acita.

6. *Kukoma mtima* - kucita zinthu zabwino osasamalira zomwe ena ali kucita.



GAWO LOYAMBA:

Ciyanjano Cioopsedwa.
(Aroma 14:19-21).

Ena aziwalo za mpingo anali ofooka ndi ena anali olimba. Ndipo Akristu olimba aja anakalipa nao Akristu ofooka aja cifukwa iwo anaganiza kuti iwo anali kumadya nyama inaperekedwa ku mafano.

Kudyatu nyama yomwe inaperekedwa ku mafano linakhala bvuto mu ufumu wonse wa Aroma. Munthu wakunja angaphe nyama yace napereka mwazi wace kapena mbali ta nyama ija nsembe kwa mulungu wace. Tsopano iye pena amatenga nyama yotsalira ija nakaigulitsa pa msika. Ndipo munthu aliyense amene anagulako sanadziwa kuti kapena nyamayi inali mbali ya nyama yomwe inatsalira pamene inaperekedwa nsembe ku milungu ya mafano. Ndipo funso linali lakuti kodi kunali kucimwa kapena iai kudya nyama yotereyi. Ena a Akristu aja anati inde kunali kucimwa kutero. Ndipo ena anati sanaona kuipa pakuteropo iai.

Paulo anacititsa nchito bvuto lotereli kuonetsa Akristu nchito yao kwa wina ndi mnzace pamene mabvuto anadzakwa iwo.

Mipingo imapangidwa ndi anthu mmodzi ndi mmodzi. Ndipo wina aliyense ali ndi maganizo ace momwe zinthu zidayenera kuti zicitidwe. Ndipo Paulo ánali kufunisitsa kuti Akristu a Ciromawa awaonetse momwe mpingo yao ungakhalire wolimba ngakhale panali kusiyana siyana pakati pa anthu. Paulo anafuna kuti Akristu omwe sanaona kuti panali be coipa kudya nyama ija amvesetse zomwe Akristu enanso anali kuganiza. Paulo anafunsa, "Cifukwa ciani mucita ciweruzo kwa abale anu? Pakuti ife tonse tidzaima ku mpando wa ciweruzo wa Mulungu.

GAWO LACIWIRI:
Nchito Yathu Tiri Nayo Kwa Akristu Anazathu a Mu Mpingo. (Aroma 14:13-18).

Penatu mkangano wa ukuru unakula pakati pa anthu omwe anaphunzitsa kuti panalibe kucimwa pakudya nyama yotereyi ndi ao amene anaphunzitsa kuti koteroko kunali kucimwa. Mbali ina ndi ina inali kumaweruza ena ndipo ciyanjano ca mpingo cinali kuonongeka.

Akristu leronso ali ndi ziganizo zosiyana pa zonga zakuti kodi zabwino ndi zoipa zomwe Mkristu angacite nzotani. Paulo akuti, "Ndidziwa ndipo nsakhazikika mtima mwa Ambuye Yesu, kuti palibe cinthu conyansa pa cokha; koma kwa ameneyo aciyesa conyansa."

Paulo atiuza kuti tisamasankha kuti cinthu ndi cabwino kapena coipa cifukwa cinthuzo sicitipweteka ife ai. Koma tidzisankha poyambirira kuona kuti pena ncopweteka kwa ena. Akristu adzikondana wina ndi mnzace, ndipo pa zonse ticitirana wina ndi mnzace zidzicitika cifukwa ca cikondi.

Nthawi zonde pali anthu amene amayang'ana zonse zimene tiri kucita. Pamene ticita zinthu zina zomwe iwo sanatsimikiza mtima kuti ziri zabwino kapena iai, pomwepo iwonse amadzicita, penatu tingawapangitse iwo kucita zinthu zina ziri zoopsa ndi zopweteka kwambiri kwa iwo. Paulo atiuza kuti tisacita kanthu kena kali konse zomwe zingacititse wina yemwe Kristu anamufera kuti aonongeke.

Paulo atiuza kuti, ngati ticita kanthu kena komwe kadzakhumudwitsa mnzathu mu



3. *Kukhumba Zonyansa* - cimo la munthu wina aliyense amene khala monga momwe afunira iye mwini osasamalira kanthu kali konse, sasamala kuti Mulungu kapena munthu aganiza ciani za zomwe ali kucita.

4. *Kupembedza mafano* - kupembedza mafano omwe anapangidwa ndi manja a munthu, kapena kanthu kena kali konse kanapangidwa ndi munthu mmalo mwa momwe cidapangidwa ndi Mulungu.

5. *Nyanga* - iyi inali mbali ya moyo wa cikunja, koma sinayenera kukhala mbali ya moyo wa Cikristu.

6. Mandano - cizondi ca munthu wina ndi mnzace. Mkristu akonda anthu onse.

7. *Ndeu* - kucita m'kangano ndi mabvuto nthawi zonse kumafuna m'tsutsano.

8. *Kaduka* -anthu omwe anasiya mpingo wina mokwiya nakaya mba mpingo wina.

9. *Zotetaba* - cilakolako cakufuna kukhala nazo koposa anthu ena.

10. *Kupsa mtima* - ukali wosaweruzika womwe umaononga m'malo mwa kupanga (kulenga).

11. *Magawano* - kuphunzitsa zinthu zomwe ziri zotsutsana ndi malemba ndi kumanena kuti ziri zoona.

12. *Njiru* - loipisitsa la macimo onse, mkhalidwe wa mtima woipa, kuzondana ndi omwe ali ndi zinthu zoposa zomwe iwe uli nazo.

13. *Kupha* - kupha aliyense.

Kodi ufulu umenewu utanthauza ciani? Kodi zitanthauza kuti tiri ndi ufulu wakucita ucimo ndi kucita monga momwe tifunira? Pamene munthu ali wa uflul ku lamulo amatsatira zofuna za thupi kapena amakakamizidwa kapena kutsogozedwa ndi mphamvu zina za pamwamba. Mkristu ayenera kumakondana ndi abale ace ndi kulola moyo wace kuti utsogozedwe ndi cikondi, cifundo ca anthu ena. Cikondi cimeneci ndico ciyenera kumalowa m'malo a zilakolako za ucimo. Pansi pa Lamulo munthu ayenera kumacita zinthu za bwino, ngati munthu alidi Mkristu weniweni, cikondi cimalamulira moyo wace - amakondwera mukukonda ndi kutumikira anthu anzace.

GAWO LACIWIRI:
Zilakolako Za Thupi.
(Agalatiya 5:16-21).

Mu mavesi amenewa Paulo atiuza zomwe zimacitika pamene tagonjera ku zilakolako za thupi. Paulo ali kucula zina za macimo a thupi.

1. *Dama* - cinali kubvomerezedwa ndi dziko la cikunja. Ndipo Cikristu cinadza nicininkha tanthauzo la tsopano la umuna ndi akazi. Cikristu ciphunzitsa kuti kukhala pa malo amodzi ndico cinthu comwe ciyenera kumacitidwa mwa ulemu ndi wolemekezeka womwe uyenera kumacitidwe ndi mwamuna ndi mkazi wa iye mwini.

2. *Codetsa* osati kukhala osayera m'khalidwe wa amuna ndi akazi kokha komanso mu moyo wonse. Codetsa catanthauza ciri conse comwe cipangitsa munthu kukhala wodetsedwa kuti sangayende ndi Mulungu. Citathauza kudetsa moyo pakucita zinthu zosayenera ndi kuganiza zosayenera. Ndi cinthu cina ciri conse comwe ciri ca dothe.



njira ya moyo wace wa Cikristu tilakwa kwambiri. Ngati ine ndipita ku nyumba ya mowa ndipo mbale wanga wa cimuna kapena wa cikazi andiona ine, ndipo iyense napita yakha naturukamo woledzera mowa, ici ndi cifukwa ca ine. Ine ndinamuuza ndi zocita zanga kuti cinali cabwino kupita ku nyumba ya mowa. Pena munganene kuti izi sidzingacitike. Mulakwa ngati muganiza ZOTERO.

Pali munthu wina mu umodzi wa mipingo yathu yemwe anali mu dikoni m'mudzi mwao. Iyeyu anadza kuno ku matauni ndipo anapeza ndhito yabwino kwambiri mu mgodi. Iyeyu amafika ku calici pafupi Sande ili yonse, koma pena pakati pa mlungu amapezeka ali nyumba ya mowa kapena mu kalabu ya anthu amene agwira nchito mu mgodi (Mine Club).

Tsiku lina wina wa Akristu athu a cinyamata anamuona ali mu nyumba ya mowa, ndipo iye anaganiza nati, "Bambo uje ndi uje mapita ku nyumba ya mowa cotero, ndi inthu cabwino kupitamo nanenso." Sipadapita miezi yambiri kuti nyamata juja akhale cakolwa. Iye anali kumacita kanthu kena kali konse, ngakhale kuba, kuti apeze tindarama pang'ono cabe tokagulira mowa. Kodi ndani amene anasoceretsa mnyamatayu?

GAWO LACITATU:
Mudzikondana Wina Ndi Mnzace.

Cikondi ndi mvano sidzingooneka m'mipingo mwathu ai. Tiyenera ku magwira nchito kuti tikhale nazo. Mtsogoleri ali yense ndi ciwalo ca mpingo ciri conse ali ndi nchito yakusungitsa mtendere mu mpingo. Mwa msanga pamene tiona bvuto ladza mu mpingo tidzikomana pamodzi, kulipempherera bvuto ndi kufunsa Mulungu kuti atithandize kulipambana bvutolo.

Ciyanjano ciri ndi mtengo wapatari ndi wofunika kwambiri mumpingo. Anthu amitundu yonse ndi mafuko onse, anthu onse kapena olemera kapena osauka, akhoza kukhala naco ciyanjano cimodzi ngati ali a mtima umodzi. Cikondi ca Mulungu cimaswa makoma olekanitsa onse pakati pa anthu. Anthu amisinkhu omwe abwenzi ao anawasiya amapeza ciyanjano mu mpingo. Anyamata ndi atsikana omwe amakomana ndi mayesero ambiri tsiku ndi tsiku akhoza kupeza cilimbitso ndi kuuzirifwa kucokera mu mpingo. Akristu ambiri atsopano angatayike popanda ciyanjano ca mu mpingo. Mpingo womwe uli naco cikondi cotereci, m'mcano ndi ndi ciyanjano udzakhala mpingo wokola miyoyo. Komwe anthu sali amu mpingo (Kristu) aona ndi kumva za mpingo wodzala ndi cikondi ca Kristu, naonso amfuna kukhala mbali ya mpingo woterowo. Mpingo wodzala ndi cikondi ungakhale cida cacikuru koposa cakukola anthu ena otayika kuti adze kwa Kristu.

GAWO LACINAI:
Ciyanjano Pamodzi Ndi Kristu.

Kristu anatilonjeza kuti, "Pomwe pali awiri kapena atatu kusinkhanira mu dzina langa Ine ndiri pakati pao." Kristu amadziziwitsa yekha kuti alipo mu ciyanjano pamene tiri kuganizira, kulankhula, ndi kumakambirana pamodzi za zinthu za Mulungu.

Pamene muli ciyanjano coonadi mu mpingo, Akristu amapitilira kumakula. Paulo atiuza kuti tonsefe tiri mmodzi mwa Kristu. Muno mulibe Myuda, kapena Mhelene, muno mulibe kapolo kapena mfulu, muno mulibe mwamuna kapena mkazi; pakuti muli nonse mmodzi mwa Kristu. (Agalatiye 3:28). Kwa Kristu tonsefe tiri cimodzimodzi. Cinthu



PHUNZIRO 8

CIKHALIDWE CATHU CA UCIMO

Nthawi yathu ndi Mulungu:

Nyimbo ya Azimai ndi vesi:

Vesi loloweza: *"Ngati tiri ndi moyo ndi Mzimu, ndi Mzimunso tiyende."* *Agalatiya 5:25.*

Lemba lowerenga: Agalatiya 5:13-26.

Pemphero:

MTSOGOLERI:

Lero dziko la Zambia ndi mbali zina zambiri za dziko lapansi ziri m'mabvuto oopsa kwambiri - m'makhalidwe. Anthu ali kuledzera koposa kale lonse; maukwati ali kulephera koposa kale lonse. Kuba kwa khala cinthu comwe cioneka tsiku ndi tsiku.

Lero tifuna kuganiza za kufooka kwathu kwa thupi ndi kuphunzira momwe mphamvu ya Mulungu ingatithandizire kupambana kufooka kumeneku.

GAWO LOYAMBA:
Bvuto Laufulu Wacikristu.
(Agalatiya 5:13-15).

Paulo ali kutiuza ife tonse kuti tiri pansi pa lamulo - mwamuna ali yense, mkazi, mnyamata ndi mtsikana - kufikira titalandira Kristu monga Mpulumutsi wathu. Pamene talandira Kristu monga Mpulumutsi wathu tilamulidwa ndi cisomo ndi cikondi ca Yesu Kristu. Izi zitanthauzatu kuti tsopano sitiri omangidwa ndi lanulo.

MTSOGOLERI:

Akristu amakula kupyolera mu utumiki wakutumikira Ambuye. Pamene tilephera kutumikira tilephera kukula monga momwe ana amalepherera kukula bwino ngati saloledwa kuti adzisunthasuntha ndi kuyendayenda.

Pempherani kuti Ambuye athandize wina aliyense wa ife kukhala mtumiki wace wa bwino.



cacikuru ncakuti munthu aliyense ndi mwana wa Mulungu kupyolera mwa cikhulupiriro mwa Kristu. Pamene ici cioneka tiri naco ciyanjano coonadi.

Paulo penatu ananenapo kuti ngakhale munthu akhale woyera kapena wakuda, wofiira, wacikasu kapena wofirira, kapena munthu ali wacuma kapena wosauka, kapena ali mu African kapena M'merican, kapena ndi mnyamata kapena wokalamba - cinthuzi ziribe kanthu mu ciyanjano ca Cikristu.

MTSOGOLERI:

Tiyeni tipemphere lero kuti mpingo wathu udzapitilira kukula ndi kukhala wolimba. Tipemphere kuti pamene mabvuto athu adza mu mpingo wathu cikondi ca Kristu cidzikhala colimba koposa kotero kuti mabvuto oterewa adzapambanidwa.

## PHUNZIRO 6

### KRISTU AMAKULA KUPYOLERA MU KULAMBIRA

Nthawi yathu ndi Mulungu:

Nyimbo ya Azimai ndi vesi:

Vesi loloweza: *"Mulungu ndiye mzimu; ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira mu-mzimu ndi m'coonani." Yohane 4:24.*

Lemba lowerenga: Marko 1:35.
Macitidwe 2:46,47.
Ahebri 10:19-25.

Pemphero:

MTSOGOLERI:

Mu nkhondo ija Yoyamba ya dziko lonse mwana wa cifumu wa ci Indian anafunsa m'American wina. "Kodi udziwa cifukwa cace comwe Mulungu ali kulangira Akristu powalola kumenyana ndi kumaononganа wina ndi mnzace monga ali kucitira?" Mwana wa mfumu uja anapitirizabe, "Ngati ndinganyozere cipembedzo canga monga momwe Akristu ambiri ali kucitira ndi zipembedzo zao ndinayenera kuyembekeza kuti Mulungu adzandinayenera kuyembekeza kuti Mulungu adzandilanga". Mwana wacifumu uja anauza m'Merica uja kuti ngakhale ziri kuti mmodzi wa ancito ace a nchito za boma mwa anthu zana limodzi anali a Ngelezi (British), anali kumatseka maofesi ace pa tsiku la mulungu liri lonse. Iye anamanganso nyumba zopempherera ziwiri za Cikristu kuti ancito a Cikristuwa naonso akhale nao malo opempherera ndi nthawinso ya kupemphere. Iye anati, "Koma amacita misonkhano



GAWO LACINAI:
Palibe Kukula Popanda Kutumikira.

Yesu ananena fanizo la matalente. Munthu wina analandira talente limodzi. Ndipo iye anacita mantha kuti angaiononge ndipo cotero anaitenga naikumbira pansi. Ndipo cotero talente lija silinapindule kanthu kwa munthu aliyense. Ndipo awiri ena analandira matalente ndipo iwo ana wagwiritsa nchito kuti apindule matalente ena a mbuye wao.

Munthu woyamba uja anali ndi talente lomwe lija pamene mbuye wace anafika.

Moyo ndi talente (mwai wakukhoza kucita zinthu) sidzinaperekedwe kwa ife kuti tidzibise kapena kuti tidzigwiritse nchito ya kwa ife tokha; komatu anaperekedwa kwa ife cifukwa ca kanthu kena koti tiwacititse. Ndipo colinga cace ncakuti titumikire Ambuye ndi matalente omwe anatipatsewo. Pamene tilephera kuwagwiritsa nchito matalentewa kuli kwabwino kuwabisa cabe cifukwa satipindulira kanthu kapena kupindulira Ambuye.

Cifukwa ceniceni ca moyo wathu ndico cakuti titumikire. Pamene tilephera kutumikira, miyoyo yathu iri yopanda kanthu mkati mwace.

Tiyenerera kukhala okondwera ndi oyamikira kwambiri kuti Mulungu sanasankha anthu ena cabe omwe angamamutumikire. Wina aliyense wa ife ali nao mwai wakumtumikira iye. Dalitso lotani nanga!

tsiku la Mlungu (Sande) mmawa basi. Anthu amenewa ali ndi cimwemwe cocepa kwambiri m'moyo wao wa mu mpingo. Awo amene apeza maora ambiri pa mlungu pakucita za bwino kwa anthu ena m'banja la mpingo ali Akristu okondwa kwambiri. Timatumikiratu Ambuye pamene tiri kutumikira anzathu. Mpingo uli nayo nchito yomwe uyenera kucita ku dziko lapansi, dzikotu liri losowa ndipo ndi mpingo wokha womwe ukhoza kupereka thandizo la cosowaci.

Cinthu cotsiriza comwe Paulo atiuza m'mavesi amenewa ndi ici: limbikani cilimbikire m'kupemphera, patsani zosowa oyera mtima, cezerani aulendo.

GAWO LACITATU:
Mkhalidwe Wa Cikristu Ndi
Anthu akunja.
(Aroma 12:14-21).

Mavesi amenewa atiuza momwe tingamacitire kwa anthu ena. Paulo anadziwa kuti nthawi zonse tidzakhala nao anthu ena omwe adzatsutsana nafe. Paulo atiuza kuti tidzikhala mwa mtendere. Tisamapweteka anthu ena tisawapweteka iwo m'maganizo pena mthupi. Ngakhale wina atipweteke ife tisabwezera kupweteka ai. Ici siciri cofewa nthawi zambiri, koma tiyenera kumacicita. Njira yokha yomwe tingacite ndiyo yakupempha Yehova kuti atithandize.

Ndi cilengedwe kwa ife ca "kubwezera" pamene munthu wina atipenya. Ncacilengedwe kudana naye munthu yemwe atida ife, koma monga Akristu tiyenera kumacita izo ziri zabwino ndi zolandiridwa pa maso pa Mulungu. Monga Akristu tiyenera kumakondana nao adani athu.



kamodzi pa miezi itatu." Ndipo m'Merica uja anamufunsa nati, "Nanga amapita kuti pa tsiku la mlungu?" Mwana wa cifumu uja anayankha nati, "Amapita kukasaka, kusewera ndi ngalawa m'madzi, kusewera mpira wa tenesi, kuthamanga ndi ngamila zao ndi kusewera njuga. Ndipo ngati ungadifunse kuti ndi cifukwa ciani Mulungu ali kulangira mitundu ya Akristu, ndiganiza ndi cifukwa cakuti iwo salambira Mulungu wao."

Kodi anthu amene sali Akristu mu mtundu wathu angafunse funso loteri za ife? "Cifukwa nciani anthu amu Zambia salambira Mulungu wao?"

Lero tifuna kuti tione zomwe kulambira koona kungatanthauze ndi kucita kukhala mbali yofunika kwambiri ya miyoyo yathu.

GAWO LOYAMBA:
Yesu Analikulambira Mwa Mtseri.
(Marko 1:35).

Ndipo Yesu anali kunka mamawa kumalo apayekha kukapemphera kusanace. Yesu kawirikawiri anali kumacita mapemphero ace nthawi ya mmawa. Akristu ambiri apeza kuti iyi ndi nthawi yabwino koposa yakulankhula ndi Mulungu. Pa nthawi ya mmawa naganizo athu amakhala ali osatanganidwa. Tifunikanso mphamvu ya mzimu poyamba zincito zathu za pa tsiku ndi tsiku.

Tiuzidwa kuti Yesu anapita ku malo apayekha kukapemphera. Pena tinganongone pemphero pa gulu la anthu. Koma ndi cinthu koposa kukhala pa malo acete kupemphera pomwe palibe zina zomwe ungamaziyang'ane ndi zomwe zingakuleketse pakati pemphero lako. Cotero Yesu anapeza malo acete kapena "apayekha" ndipo komweko analankhula ndi Mulungu.

Pemphero ndilo mbali yopambana koposa ya kupembedza. Sitidziwa kuti Yesu anali kupemphera nthawi ya itari bwanji. Sotidziwanso kapena anali kugwada pansi. Sitidziwanso ngati anapemphera molimba (momveka). Zinthu zoterezi siziri zofunika kwenikweni ai. Cinthu cofunika kwambiri ndico cakuti Iye analankhula ndi Mulungu. Yesu anali kuyembedezera mwa kacetecete kulola Mulungu kuti alankhule naye mu nthawi ya kupembedza mwamtseri. Cipangano citiuza za nthawi zina zambiri zomwe Yesu anacoka kunka kukapemphera. Mu nthawi zimenezi zakupempherazi analandira mphamvu ndi nzeru zakucitira nchito yace.

GAWO LACIWIRI:

Mpingo Womwe Umapembedza.
(Macitidwe 2:46-47).

Akristu atsopanowa anali Ayuda, ndipo pa nthawi yoyambayambayi anali kumapembedza mu Kacisi. Posacedwa tiona kuti misonkhano ya mpingo iri kucitidwira panja pa sunagoge wa Ayuda. Uwu unali msonkhano wa pa gulu wacipembedzo. Cioneka kuti anthuwa anali kumapita ku Kacisi tsiku ndi tsiku. Posacedwa anayamba kumacita misonkhano yao yamapemphero pa tsiku la Mulungu, tsiku loyamba la mulungu, cifukwa linali tsiku la cikumbukiro ca kuunka kwa akufa kwa Yesu. Kalekale nyumba zopempherera zisanamangidwe, mipingo inali kumakomana kucita msonkhano wa kupembedza pamodzi.

Cimwemwe, ndi cikondwerero, ndi mtenderewomwe unaoneka mwa Akristu oyambawa zinaoneka kwa anthu omwe sanali amumpingo kuona zinthu zazikuru. Mzimu woyera anali nao Akristu amenewa ndipo tiuzidwa kuti Ambuye anaonjezera kwa iwo ambiri tsiku



ndi kunyada kotereku sali olandiridwa pamaso pa Mulungu. Aliyense wa ife adayenera kuyesa moyo wace ndi moyo wa Yesu Kristu. Pamene titero tidzaona kuti ife tokha tiri cabe. Yesu yekha ndiye ali wabwino ndi wa ngwiro.

GAWO LACIWIRI:

Kutumikirani Wina Ndi Mnzace
Kwa Akristu.
(Aroma 12:9-13).

Paulo anayamba ndi cikondi. Cikondi ndico comwe ciri mbali yopambana ya cilengedwe cathu ca umunthu. Cikondi cimalenga mpingo ndi kuupanga kumapitabe pa tsogolo. Cikondi cidzikhala m'mitima mwa ana a Mulungu.

Paulo atiuzanso ktui atiuzanso kuti coipa. Tidzidana naco coipa ndi zonse zakucita coipa. Koma tidzikangamira pa zinthu zomwe ziri za bwino.

Tiyenera kukhala naco cikondi ca cibale. Mu mpingo ciwalo ciri conse ciri nayo nchito ya kukondana ndi Mkristu mnzace. Mpingo ndiwodi banja la Mulungu; ndipo cotero monga abale ndi alongo mwa Kristu tiyembekezedwa kukondana wina ndi mnzace. Tidzikhalanso okhulupirika kwa wina ndi mnzace monga abale ndi alongo mwa Kristu.

Tisamaiwala kuti monga Akristu, nchito yathu ndiyo ya kutumikiraosati kutumikiridwa. Ndi cinthu capafupi kuganiza zomwe banja lathu la mpingo lingacite kwa ife, koma kodi ifeyo timaganizirapo zomwe tingawacitire? Alipotu anthu ena amene amaganizira kuti nchito yao monga Akristu ndiyo yakumacita nao misonkhano ya pa

kuru ca Mulungu comwe cinatipatsa ife cipulumutso, tidzakhala nayo nchito kwa iye. Cifukwa ca zonse zimene Mulungu anaticitira tiyenera kuonetsa kuyamikira kwathu pomutumikira.

Paulo akuti, "Perekani matupi anu." Tiyenera kupereka matupi athu monga mphatso ya thunthu, kapena nsembe, kwa Mulungu. Sitifunikanso kuti tidzipereka nsembe yakufa pa guwa lwansembe monga momwe zinali kufunikira mu Cipangano Cakale ai. Copereka cathu ndico thupi lamoyo monga nsembe. Thupi la munthu ndi Kacisi wa Mzimu Woyera. Zonse zimene munthu angacitire Mulungu ziyenera kucitidwa ndi thupi. Nchito zathu m'mabanja, pa m'godi, ku ofesi - zidziperekedwa kwa Mulungu. Moyo wa tsiku ndi tsiku ndi nsembe ya moyo.

Ngati tingapereke kanthu kali konse kamene tikacita kwa Mulungu - nchito yathu yonse, masewera ndi kupembedza, tiyeneratu kusintha njira zathu zina zomwe tikhaliramo. Ngati nchito yathu, maphunziro athu ndi masewera athu ali mu zinthu zina zomwe sidzilandiridwa kwa Mulungu tiyeneratu kudzileka izo. Kodi mungapereke ziri zonse omwe mulankhula ndi kucita tsiku liri lonse kwa Mulungu? Ngati sitero muyenera kusintha zina za njira zanu.

Paulo anadziwa kuti anthu ambiri amaziganizira za iwo ena koposa momwe akadamacitira. Anthu ena amaganza kuti iwo ali opambana koposa anzao ena onse ndiponso amaganiza kuti zonse zomwe iwo angacite ziri zabwino koposa zomwe zingacitidwe ndi munthu wina aliyense. Paulo anticenjeza kuti tisanyada tere. Anthu amene ali ndi maganizo amtundu uwu anayenera kudzionanso okha poyesa miyoyo yao, cifukwa pamene ali



ndi tsiku ao amene anali kupulumutsidwa. Pamene Ambuye aonjezera anthu ku mipingo yathu palibe cifukwa cakumadera nkhawa za iwo. Mpingo wokha womwe upemphera, ndi kupembedwa ndiwo ungakope anthu kudza kwa Kristu.

GAWO LACITATU:

Timafuka Kwa Mulungu Kupyolera Mwa Kristu. (Ahebri 10:19-25).

Buku la Ahebri linalembedwa kwa Akristu a Ciyuda omwe anali kukakamizidwa kuti acoke mu Cikristu kubwerera ku Ciyuda (cipembedzo ca Ciyuda). Mlembi wa Ahebri awauza anthuwa zonse za kuposa kwace kwa Cikristu ndi Cipembedzo ca Ciyuda. Awauza momwe Yesu aliri wamkuru ndi woposa aneneri angelo, Mose, ndi Aaroni. Yesu ndiye anali nsembe ya ngwiro.

Iye anena kuti zinthu zonse zinacitidwa kuti zikhale zotheka kwa munthu ali yense kukhala njira ya ngwiro yakufika kwa Mulungu.

Munthu sali wantengo wakuti angafike pamaso pa Mulungu, koma ngati moyo wace wapangidwa kukhala wangwiro ndi Yesu Kristu, akhoza kunka kwa Ambuye wace. Ndipo cotero tingapembedze Mulungu yekha kupyolera mwa mphamvu yakutsuka ya Yesu Kristu.

Tisamakaikira cikhulupiriro cathu mwa Kristu. Tiyenera kumaimira Yesu Kristu pa dziko lonse lapansi. Cikhulupiriro comwe cimakopa ena cidzikhala cotsimikiza, coona ndi cotsimikiza mu mtima. Pa malo pomwe pakhala Akristu munthu aliyense azizindikira nchito yace kwa anthu ena. Ife tiyenera kumakhala citzanzo ca cikondi ndi nchito zabwino.

GAWO LACINAI:
Kupembedza kwa pa Banja.

Mtundu wina wa kupembedza ndiwo wakupembedza kwa pa banja. Banja liri lonse la Cikristu lidzikhala ndi nthawi ya kupembedza pamodzi. Iwo adziwerenga cipangano cao pamodzi, kupemphera pena ndi kuyimba zolemekeza Yehova. Tiuzidwa kuti, "Banja lomwe limapemphera pamodzi, limakhala pamodzi. Nzoona kotani bwanji. Ngati anyamata omwe angokwatirana akadamayamba kupembedza kwa pabanjaku m'mabanja ao sipakadakhala kulekana kwa maukwati ndi mabanja osweka.

Tidzikumbukira kuti Cipangano ciri cofunika kwambiri mu mapembedzo oterewa - am'tseri, mbanja ndi pagulu. Mtima wa kupembedza ndiwo pemphero.

Cipangano, pemphero ndi mtima wolola ndizo zinthu zitatu zofunikira za kupembedza.

MTSOGOLERI:

Kupembedza ndiyo mbali yofunika kwambiri ya moyo wa Cikristu. Popamba kupembedza tingakhale Akristu opanda pace. Tiyeni tidzikhala okhulupirika m'mapembedzo athu. Yambani mapembedzo a pa banja m'banja lanu lero ndikuti muone dalitso lomwe angakutengereni m'moyo mwanu.



PHUNZIRO 7

KUKULA MWA CIKRISTU KUPYOLERA
MU KUTUMIKIRA

Nthawi yathu ndi Mulungu:

Nyimbo ya Azimai ndi vesi:

Vesi loloweza: *"Pakuti ndithu Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa, koma kutumikira, ndikupereka moyo wace ndipo la kwa anthu ambiri."*
*Marko 10:45.*

Lemba lowerenga: Aroma 12:1-13.

Pemphero:

MTSOGOLERI:

Kwa milungu yowerengeka yapitayi takhala tiri kuphunzira za kakulidwe monga Akristu. Taphunzira za kukula m'Cikristu kupyolera m'zobvuta, m'ciyanjano, m'kulambira, zonsezi nzofunika ngati wina afuna kuti atumikire Ambuye.

Lero tidzaphunzira Mutu wa 12 wa buku la Aroma womwe utiuza ife momwe tingatumiona zomwe zitanthauza kutumikira Ambuye kwenikweni ndi momwe utumikiwu ungatithandizire kukula monga Akristu.

GAWO LOYAMBA:
Utumiki Woyenera.
(Aroma 12:1-3).

Paulo ali kutiuza m'mavesi amenewa kuti cifukwa ca cifundo ndi cisomo caci-